Chisindikizo Chachiwiri


Usiku wabwino, abwenzi. Tiyeni tonse tiyime kwa mphindi chabe kwa pemphero, ngati inu mungathe.

2 Atate athu Akumwamba, ife tasonkhananso mu msonkhano waulemu uwu, usikuuno, mu utumiki wa Ambuye. Ndipo Inu munalonjeza kuti paliponse pamene ife tidzasonkhane limodzi, ochuluka monga awiri kapena atatu a ife, kuti Inu mukanadzakhala pakati pathu. Ndipo ife tikhoza kukhala otsimikizika kuti Inu muli pano, pakuti ife tasonkhana mu Dzina Lake.

3 Tsopano ife tikupemphera, Atate, kuti—kuti Inu mubwere usikuuno ndipo mudzamatule Chisindikizo Chachiwiri ichi kwa ife. Ndipo monga a—wandakatulo wanena, kuti iye akanafuna atayang'ana kupyola katani la nthawi. Ndipo ndicho chokhumba chathu, Ambuye, ndicho basi ku—kungoyang'ana mopyola ndi kuwona chimene chiri patsogolo. Ndipo ife tikupemphera kuti Mwanawankhosa yemwe anali ataphedwa, abwere pakati pathu tsopano ndi kudzamatula Chisindikizochi, ndi—ndi kudzaulula Icho kwa ife, zinthu zimene ife tikusowa kuziwona.

4 Pali ena pano, Ambuye, amene sanalowebe mu chiyanjano chachikulu ichi pozungulira Khristu. Ife tikupemphera kuti, usikuuno, kuti iwo apange kusankha Kwamuyaya uko, kuti adzazidwe nawo Mzimu wa Mulungu.

5 Ngati pali aliyense wodwala, Atate, ife tikupemphera kuti Inu muwachize iwo. Pali mipango yambiri imene yaikidwa apa imene ine ndaikapo manja anga, pokumbukira za—za Baibulo, za Paulo Woyera, pamene iwo ankatenga kuchokera mu thupi lake mipango ndi zovala. Mizimu yoipa inkawachokera anthu, ndipo iwo ankachiritsidwa.

6 Ife tikuwona kuyandikira kwa Kudza kwa Ambuye. Ife tikudziwa kuti nthawi ikuyandikira. Zinthu izi zabwereranso kachiwiri ku Mpingo, zitapita zaka naintini handiredi.

7 Tsopano ife tikupemphera, Atate, kuti Inu mupereke zinthu izi zimene ife tikuzipempha. Mulimbikitseni wantchito Wanu, ndipo muthandize antchito Anu kulikonse, Ambuye, ndipo makamaka ife amene tasonkhana pano usikuuno, kuti ife tikhoze kulandira Mawu. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Ameni.

8 Ndithudi nkwabwino kubwereranso mnyumba ya Ambuye kachiwiri usikuuno. Ndipo ine ndikudziwa kuti ambiri a inu mwaimirira, ine—ine ndikupepesa chifukwa cha zimenezo, koma palibenso china choposa chimene ife tingachite. Ife—ife

tiri nacho—tchalitchi monga ngati . . . tinachiwonjezera icho kufika pamene ife tingatenge atatu kapena foro, firii handiredi kapena foro handiredi ochulukirapo mkati muno. Koma mmisonkhano yapadera yonga iyi, icho—icho chimanyamula gulu lochulukirapo pang'ono.

9 Tsopano, oh, ine ndikungokhala ndi nthawi yopambana, kupemphera, ndi kuwerenga izi—Zisindikizo izi. Ine ndikuyembekeza kuti inu nonse mukutero, nanunso. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ine—ine ndikutsimikiza kuti inu mukutero. Ndipo ngati Ziri zatanthauzo kwambiri kwa inu monga momwe Izo ziriri kwa ine, izo ndithudi . . . inu mukukhala nayo nthawi yopambana. Ndipo ine ndiri ndi . . .

10 Ine ndikufuna kumuimbira bwenzi wanga wamkazi, ukatha msonkhanowu. Ndipo ili ndi tsiku lake lobadwa. Iye wakwanitsa usinkhu wa zaka thwelovu lero, Sarah, mwana wanga wamkazi. Ndipo wotsatira, kenako, likadutsa mawa, ine ndidzayenera kupanga kuyimba kwina, chifukwa lidzakhala tsiku la kubadwa kwa Becky.

11 Ndipo tsopano, usikuuno, ife tikuphunzira Chisindikizo Chachiwiri ichi. Ndipo kwa Zisindikizo zinayi zoyambirirazo pali okwera pakavalo anayi. Ndipo ine ndikukuuzani inu, lero chinachake chachitikanso. Ndipo, ine—ine, chinachake chimene ine . . . Ine ndinapita ndi kukatenga zolemba zakale zomwe ine ndinali nazo, zomwe ine ndinaziyankhula, kalekale, ndipo ndinangokhala pansi pamenepo. Ndipo ine ndinaganiza, "Chabwino, ine—ine ndinachita chopambana chimene ine ndikanatha." Ndipo olemba ambiri ndi zinthu, ndipo ine ndinaganiza, "Chabwino, ine ndiwerenga kanthawi pang'ono, ndi kuyang'ananso ndi kuwona *ichi* ndi *icho*." Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, chinachake chimangochitika, ndipo icho chonse ndi chosinthika. Icho chimangobwera mosinthika. Ndiye ine ndimatenga pensulo mofulumira pomwepo, ndi kuyamba kulemba mwamsanga basi momwe ine ndingathere, Iye adakali pamenepo.

12 Oh, chinachake chinachitika basi kwa pafupi ora ndi theka lapitalo. Ine ndimamuuza M'bale Wood, tikubwera kumeneko, maminiti pang'ono chabe apitawo. Chinachake basi, inu mukudziwa. Inu mukudziwa, pali zinthu zambiri zimene zimachitika, zomwe iwe sungaziyankhule basi, inu mukudziwa. Koma basi chinachake chinangochitika chimene changondithandiza ine kwambiri.

13 Ine ndiri naye mzanga muno penapake mchipindachi. Ndithudi, nonsenu ndinu abwenzi anga. Uyu—m'bale uyu ndi M'bale Lee Vayle. Iye ndi m'bale wofunikira, ndipo wophunzira weniweni wa Malemba. Dr. Vayle ndi wa Baptist wokhala ndi Mzimu Woyera. Ndipo iye ndi . . . Ine sindikunena izi moyamikira, ine ndikungonena izi chifukwa ine

ndikuzikhulupirira izo. Ine ndikuganiza kuti Iye ndi m'modzi mwa ophunzira odziwa bwino kwambiri omwe ndimawadziwa, m'magulu athu. Ndipo iye anangondilembera ine kapepala kakang'ono apa, ndipo kanatumizidwa mmenemo ndi Billy. Ndipo Billy samakwanitsa nkomwe kukafikitsa iko, kwa ine. Ndipo ine ndikuganiza...Ine sindinakawerenge iko konse, koma ine ndimati ndingonena zimene iye ananena apa. Ndipo ine ndinangowerenga izo, M'bale Vayle, ngati inu muli pano. Ine ndinangowerenga izi pafupifupi miyezi sikisi yapitayo.

14 "Ine sindikutsimikiza," Iye anatero. "M'bale Bill, ine sindikutsimikiza, koma ine ndikukhulupirira kuti Polycarp anali wophunzira wa Yohane Woyera." Uko nkulondola. Iye anali. "Ine ndikuganiza kuti Irenaeus anali wophunzira wa—wa Polycarp." Ndiko kulondola, ndendende. "Irenaeus anati, 'Yesu adzabwerera—adzabwerera pamene membala wosankhidwa wotsiriza wa Thupi la Khristu adzabwere mkati.'"

15 Ameneyo anali Irenaeus, pafupifupi zaka foro handiredi pa...itachitika imfa ya Khristu. Iye anati, "Pamene m'badwo wotsiriza uwu udzabweremo..." Tsopano, ndizo mu—Pre-Nicaea Council. Inu azimzanga pano, amene munawerenga—a...munawerenga Lemba, ndi kuwerenga a...ine ndikutanthauza, kuwerenga mbiriyakale ya Baibulo, inu muzipeza zimenezo mu pre-...mu Pre-Nicaea Council. Ndipo ine ndikuganiza kuti ndi bukhu loyamba kapena bukhu lachiwiri, inu—inu mudzazipeza izo. Ndipo tsopano, iye anaziwona izo, zaka zapitazo, pamene iye anati, "Pa wotsiriza, wotsiriza—wosankhidwa wotsiriza, wosankhidwa ameneyo."

16 Anthu amaganiza kuti kusankhidwa ndi chinachake chimene changokhala—chimene changobweretsedwa kuno posakhalitsapa. Mai! Icho ndi chimodzi cha ziphunzitso zakale kwambiri zimene ife tiri nazo: kusankhidwa ndi kuyitanidwa. Ndipo kotero Irenaeus, ndithudi, ophunzira enieni a Lemba, nthawizonse ankakhulupirira mu kusankhidwa.

17 Ndipo kotero Irenaeus anali mmodzi wa—angelo a mibadwo ya mpingo, monga ife tinawonera, monga ife tinawerengera. Ife tikukhulupirira. Ndithudi, tsopano, izo zonse zinali zinsinsi. Izo zonse ziri apa, kulondola, zabisika pomwepa mu Zisindikizo izi, inu mukuona. Ndipo izo ziri zoti ziwululidwa mu tsiku lotsiriza. Momwe izo zinayambira ndi Paulo, ndi—ndi Irenaeus, ndi Martin, ndi ena otero, mmusi, ndipo zafika mpaka mmusi ku m'badwo wotsiriza.

18 Ndipo, tsopano, ife tikudalira tsopano kuti Ambuye atidalitsa ife mu kuyesetsa kwathu usikuuno. Tsopano ife takhala...Chisindikizo Choyamba, ine ndithudi ndinasangalala nacho icho. Chisindikizo Choyamba, madalitso amene anatsagana nacho Icho, kwa ine!

19 Ndipo tsopano ine—ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu motalika kwambiri. Koma, inu mukuona, ine—ine ndikhala ndikupita tsopano kachiwiri basi, mmausiku angapo, ndipo izi zikatha. Ndipo tiyenera basi kukhala ngati tavutika kanthawi pang'ono. Ndipo ine ndikuyamikira . . .

20 Ine ndikumuwona M'bale Junior Jackson waimirira pamenepo. Ine . . . Ndipo ine ndimaganiza kuti ndinamuwona M'bale Ruddell, mphindi pang'ono zapitazo, muno penapake. Ndipo abale amenewo, ndiyo mipingo yapachibale imene yalola kubwera, ndi enawonso. Ife ndithudi tikuyamikira zimenezo. Ndipo ine ndikumuwona M'bale Hooper, ine ndikukhulupirira, waimirira cha pa khoma pamenepo, wochokera ku Utica, mpingo kumeneko. Ndipo ndithudi tikuyamikira chigwirizano chanu chonse chabwino mu izi.

21 Tsopano, usiku wathawu, monga ife nthawizonse timakondera, mu kuphunzitsa pa—pa Zisindikizo, ife timaphunzitsa izo mwanjira yomweyo imene inu mumachitira pa—pa—mibadwo ya mpingo. Ndipo pamene ife tinatsiriza kuphunzitsa m'badwo wa mpingo, nthawi yotsiriza pamene ine ndinajambula zimenezo apa pa—pa guwa, pa bolodi, ndi angati akukumbukira chimene chinachitika? Iye anabwera pansi pomwepo, anabwereranso pa khoma lomwelo, mu Kuwala, ndipo anadzajambula izo, Iyemwini, pomwepo apo pa khoma, pamaso pa ife tonse. Mngelo wa Ambuye anadzaima pomwepa apa pamaso pa anthu ma handiredi angapo.

22 Ndipo tsopano Iye ali—Iye akuchita chinachake chauzimu kwenikweni tsopano, nayenso, ndipo kotero ife tikungoyembekezera zinthu zazikulu. Ife sitikudziwa . . . Inu mukufuna kungoyembekezera izo—kuyembekezera kwakukulu kumeneko, sindikudziwa basi chimene chiti chichitike motsatira, inu mukudziwa, basi—kumangoyembekezera. Tsopano, ndi wamkulu bwanji Mulungu kwa ife, ndipo ndi wodabwitsa bwanji! Ife tikumuyamikira Iye kwambiri!

23 Tsopano, ndime ya 1 ndi ya 2, ine ndiwerenga Izo, kukhala ngati ndiyike maziko pang'ono. Ndipo kenako ife titenga ndime ya 3 ndi ya 4, kwa Chisindikizo Chachiwiri. Ndiye kenako ndime ya 5 ndi ya 6 ndi Chisindikizo Chachitatu. Ndipo ya 7 ndi 8 ndi . . . Ndime ziwiri kwa wokwera pa kavalo aliyense. Ndipo tsopano ine ndikufuna kuti inu muyang'ane momwe anthu awa . . . Pa kavalo wotumbululuka uyu, mwinamwake . . . Apa iye akubwera, akumangopitirira kusintha pamene iye akupita mmusi.

24 Ndipo kenako Chisindikizo chopambana, chotsiriza chija ndi choti chidzatsegulidwe, ngati Mulungu alola, Lamlungu likudzali usiku! Kuti, pamene icho chinachitika, apo panali basi, chinthu chokhacho chimene chinachitika, "kunali chete Kumwamba kwa theka la ora." Mulungu atithandize ife.

25 Tsopano ine ndiwerenga ndime ya 3 tsopano.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachiwiri, ine ndinamva chamoyo chachiwiri chikuti, Bwera udzawone.

Ndipo apo panatulukira kavalo wina . . . (ndime ya 4) . . . *amene anali wofiira: ndipo mphamvu inapatsidwa kwa iye amene anakhala pamenepo kukachotsa mtendere pa dziko lapansi,* . . . *kuti iwo aziphana wina ndi mzake* . . . *aziphana wina ndi mzake: ndipo kunapatsidwa kwa iye lupanga lalikulu.*

26 Tsopano, chinthu chachinsinsi tsopano, pamene cha—Chamoyocho chinamuuza Yohane, "Ingobwera ndipo udzawone." Ndipo iye sanawone chimene icho chinali. Iye anangowona chophiphiritsa. Ndipo chophiphiritsa chimenecho, chifukwa chimene icho . . . Iye anati, "Bwera, udzawone," koma iye anawona chophiphiritsa, chimene iye anali woti achiphiphiritsire kwa mpingo, mwa njira yakuti iwo akanadzachiwona; mpaka icho chitadzabwera ku m'badwo wotsiriza, ndipo zikadzatero Chisindikizocho chidzatsegulidwa.

27 Tsopano, aliyense akumvetsa zimenezo tsopano, mwaona, Zisindikizozo zidzatsegulidwa. Ndipo kodi inu simuli okondwa kuti mukukhala mu tsiku ili? Icho, mukuona, si chokhacho, amzanga, koma nthawizonse muzikumbukira tsopano, Lamlungu lapitali mmawa, pamene chinthu chonsecho chinakhazikitsidwira pa, kuphweka! Mukuona? Kuphweka, kudzichepetsa, zimachitika mwanjira yoteroyo mwakuti anthu amapita basi cha pomwepo ndipo osadziwa nkomwe kuti Izo zikuchitika.

28 Ndipo, kumbukirani, ife tikuyembekezera Kudza kwa Ambuye, nthawi iliyonse. Ndipo pamene ife . . . Ine ndinapanga neno, kuti mwinamwake Mkwatulo udzakhala mwanjira yomweyo. Udzakhala utapita, zitatha, ndipo palibe amene ati adzadziwe kanthu za zimenezo. Udzangobwera monga chomwecho. Mukuona? Ndipo kawirikawiri . . . Mungobwerera kudutsa mu Baibulo ndi kuyang'ana momwe izo zimachitikira monga chomwecho. Mukuona?

29 Ngakhale chinthu chachikulu monga kubwera kwa Ambuye Yesu, palibe amene anadziwa kanthu za icho. Iwo ankaganiza, "Chidempete chija, winawake." Mipingo inkati, "Wotentheka chabe. Ife . . . Iye ndi wopenga kwenikweni." Anati, "Iye ndi munthu wamisala." "Ife tikudziwa kuti Iwe ndi wamisala." *Misala* imatanthauza "kupenga." "Ife tikudziwa kuti Iwe uli ndi mdierekezi, ndipo iye wakupengetsa iwe. Ndiye iwe ukuyesera kuti utiphunzitse ife? Pamene, iwe unabadwira kunja uko, mwapathengo. Ife . . . Iwe unabadwira mu chiwerewere. Ukuyesera kuti uziphunzitsa amuna monga ife, ansembe, ndi ena otero, kachisi?" Chabwino, mai, icho chinali chonyoza kwa iwo.

30 Pamene Yohane anabwera, zinali zitanenedwa, kutsika kudutsa mmibadwo, kuchokera kwa Yesaya mpaka kwa Malaki. Ndizo thwelovu handiredi . . . kapena zaka seveni handiredi ndi thwelovu, iye anali atawonedwa ndi aneneri, akubwera. Aliyense anali akumuyembekezera iye kuti abwera, ankayembekezera izo nthawi iliyonse. Koma njira yomwe iye anabwerera, iye analalikira ndipo anachita ntchito yake, ndipo anapita mu Ulemelero.

31 Ndipo ngakhale atumwiwo sanadziwe izo, pakuti iwo anamufunsa Iye. Iwo anati, "Tsopano, ngati—ngati Mwana wa munthu akupita ku Yerusalemu, zinthu zonse izi, kuti akaperekedwe," anati, "nchifukwa chiyani nanga Lemba limanena kuti 'Eliya adzabwera poyamba'?"

32 Yesu anati, "Iye anabwera kale, ndipo inu simunadziwe izo. Ndipo iye anachita ndendende basi chimene Lemba linati iye akanadzachita. Ndipo iwo anachita kwa iye basi zimene zinalembedwa." Mukuona? Ndipo iwo sanakhoze kuzimvetsa izo. Iye anati, "Iye anali Yohane."

Ndipo, ndiye, "Oh!" Mwaona, iwo—iwo anadzuka, kwa izo. Iwo . . .

33 Ndipo pamene, ngakhale, potsiriza, zitatha zinthu zonse zimene Iye—Iye anali atazichita, ndi zizindikiro zomwe Iye anawasonyeza iwo, ndipo anali ngakhale atawaitana iwo. Anati, "Ndani wa inu angakhoze kunditsutsa Ine za tchimo, kusakhulupirira? Ngati Ine sindinachite ndendende basi zomwe Lemba linanena kuti udindo Wanga ukanadzachita pamene Ine ndidzabwera ku dziko lapansi, ndiye mundisonyeze Ine pamene ndachimwa. Mukuona? Ndiye ine ndiku—Ine ndikusonyezani inu chimene inu mukuyenera kukhala, ndipo tiyeni tiwone ngati inu mukukhulupirira izo, kapena ayi." Mukuona? Iye akanakhoza kubwereranso mmbuyo ndi kudzati, "Inu mumayenera kukhulupirira pa Ine pamene Ine ndinadza." Iwo sanachite zimenezo, mwaona, kotero iwo anadziwa bwino kuposa kumangiriza pa Iye, pa zimenezo. Koma Iye anati, "Ndani wa inu angakhoze kunditsutsa Ine za kusakhulupirira? Mukuona? Kodi Ine sindinachite ndendende basi chimene icho chinali?"

34 Ndipo ngakhale atumwi, akupitirira, ankapunthwa. Ife tikudziwa momwe Malemba amayendera. Kenako potsiriza, pamapeto, iwo anati, "Tsopano ife tikukhulupirira. Ife tikukhulupirira kuti palibe munthu amene ayenera kukuwuzani Inu, pakuti Inu mumadziwa zinthu zonse."

35 Tsopano, ine ndikanakonda ndikanawona nkhope Yake. Iye ayenera kuti anayang'ana pa iwo, anati, "Chabwino, kodi inu tsopano mukukhulupirira? Potsiriza kwakucherani inu." Chabwino, izo sizimayenera kukhala, mwinamwake, kufikira nthawi imeneyo, mukuona. Ndipo Mulungu amagwiritsa

ntchito chirichonse molondola basi, inu mukudziwa. Ine—ine ndimankonda Iye chifukwa cha izo.

36 Koma tsopano ife tikuganiza za m'badwo wathu tsopano. Chifukwa, ine ndikayamba kuyankhula pa izo, ife sitilowa mu Zisindikizo izi, nkomwe.

37 Ndipo tsopano, kumbukirani, ine ndikulandira zopempha zambiri za kupempherera odwala. Ndipo ndikumapempherera . . . nthawi zonse, kwa chopempha chirichonse chimene ndikumalandira, ndi kwa mipango ndi zinthu. Ndipo ngati ife tingakhoze kutsiriza Zisindikizo izi, mpaka ku Chisindikizo chotsiriza, Lamlungu mmawa ife . . . Ngati icho chingadzakhale chifuniro cha Ambuye, ife tikufuna kudzakhala nawo basi msonkhano wabwino wachikale wamachiritso muno, inu mukudziwa, pamene iwe ungatenge basi mmawa wathunthu kupempherera odwala. Ndipo ine—ndine wotsimikiza kwenikweni kuti iwo udzakhala msonkhano wa machiritso wachirendo. Mukuona? Ine ndikungokhala nako kumverera koteroko, mukuona. Ndipo kotero, osati wachirendo, koma iwo mwina ukhoza kudzakhala wachirendo pang'ono kwa ena, mwaona, chimene ine ndikutanthauza.

38 Tsopano, ndi chopambana bwanji chisomo cha Mulungu, kuwulula zinsinsi Zake kwa ife mu tsiku ili! Tsopano, ife tonse tikukhulupirira kuti tikukhala mu tsiku lotsiriza. Ife tikukhulupirira zimenezo. Ndipo kumbukirani, zinsinsizi zinali zoti zidzawululidwe mu tsiku lotsiriza. Ndipo kodi Iye amawulula chotani Mawu Ake, zinsinsi Zake? Baibulo linatero. Kodi inu mukufuna mutawerenga pamene Iye akunena zimenezo? Tiyeni tingotsegula ndipo tiwone momwe Iye amawululira zinsinsi Zake.

39 Tsopano ine ndikufuna kuti inu muwerenge ku Amosi. Mutsegule ku Bukhu la Amosi, ndipo ine ndikufuna kuti inu muwerenge mu mutu wa 3 wa Amosi, ndi ndime ya 7. Chabwino. Ine ndiwerenga ndime ya 6, nayonso.

> *Kodi lipenga* . . . lidzawomba *mu mzinda, ndipo anthu osachita mantha? kodi mudzakhala choipa mu mzinda, ndipo* AMBUYE *sanachichite icho?*
>
> *Ndithudi Ambuye . . . sadzachita kanthu, koma iye amawululira* zinsinsi *zake kwa antchito ake aneneri.*

40 Tsopano, mmasiku otsiriza, ife tiri . . . Izo zinanenedweratu kwa ife kuti kudzauka a—mneneri.

41 Tsopano, ife tikudziwa kuti takhala nawo a mitundu yonse. Tsopano, ine ndikuzindikira, nditatha kuyang'ana pozungulira usikuuno, ine—ine ndikuyankhula pano pamene ophunzira akhala, ndipo ine—ine ndikufuna kuti inu mundimvetsetse ine. Ndipo inu mukuzindikira, matepi awa akupita padziko lonse, mwaona, basi pafupifupi padziko lonse. Ndipo ine ndikanafuna kuti inu musati, mwanjira iliyonse, musaganize

kuti ine ndikuyesetsa kubairamo mtundu wina wa a—mwambo wa mabulangete a Eliya kapena mikanjo. Ndi zonse—zinthu zonse izo, ife takhala nazo zochuluka za izo. Koma, inu mukudziwa, zinthu zonsezo ziri kokha zotsogolera chinthu chenicheni chimene chikubwera, kuti chiwaponyere anthu kumbali.

42 Kodi inu mumadziwa kuti ife tinali nawo abodza—atsogoleri abodza amene anawuka, amesiya abodza, Khristu asanadze? Kodi sanati, kodi sanati . . . Mphunzitsi wa tsiku lija, mphunzitsi wopambana uja, Gamaliel, pamene a—funso linabwerapo lokhudza kuwamenya amuna awa, ndi zina zotero, iye anati, "Asiyeni iwo okha. Ngati izo ziri za Mulungu, bwanji, inu mudzazipeza nokha mukumenyana ndi Mulungu. Koma ngati siziri za Mulungu . . ." Anati, "Kodi sanawuke munthu, osati kale kwambiri, ndipo anawatengera foro handiredi kulowa nawo mchipululu, ndi zina zotero? Ife tiri nazo zinthu zimenezo." Chinali chiyani chimenecho? Zonsezo zinkatsogolera Chinthu chenicheni pamene Icho chinali kubwera.

43 Tsopano, mwaona, Satana amazidzutsa zimenezo. Penyani kuchenjera kwa munthu uyu yemwe ife tikumukamba apa, Satana, pamene ife tikumufutukula iye pomwe pano; kungomuvulira iye pansi, mwa Malemba, ndi kukulolani inu muwone yemwe iye ali. Ndicho chimene . . . chimene chikuyenera kuchitidwa.

44 Ndipo, inu mukukumbukira, iye sanayeserepo kuti alowe mmenemo ndi kukhala wachikominisi, Satana sanatero. Iye ndi wotsutsakhristu. "Woyandikira kwambiri, mwakuti," Yesu anati, "akanadzanyenga Osankhidwa omwe . . ." Ndipo ndiwo Amene anabisidwa mu Zisindikizo izi, amene maina awo ali pa Bukhu chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi.

45 Iye ndi munthu wothyathyalika. Ndipo pamene iye akuwona chinthu ichi chikubwera, chikubwerapo, ndiye iye akuponyera chirichonse chimene iye angakhoze kumeneko, kuti akachisokoneze icho chisanafike kumeneko. Kodi inu mumadziwa kuti padzakhala akhristu abodza adzawuke mmasiku otsiriza? Izo ziyenera kutsatira mwamsanga pambuyo pa uwu, pambuyo pa Uthenga wopambana uwu umene m'bale uyu adzayankhule, yemwe ati adzabwere, atadzozedwa ndi mzimu wa Eliya, mwamsanga.

46 Ndipo iwo adzamuphonya iye. Ena a iwo adzaganiza kuti iye ndi Mesiya. Koma iye mosamalitsa adzati, "Ayi." Chifukwa, izo zidzayenera kudzabweramo monga Yohane.

47 Mu nthawi ya Yohane M'batizi, pamene iye anatulukira kunja kuja kukalalikira, iwo anati kwa iye, "Kodi sindiwe Mesiya? Kodi sindiwe Iye?"

48 Iye anati, "Ine sindine ayi. Ine sindiri woyenera kumasula nsapato Zake. Koma ine—ine ndikukubatizani inu ndi madzi,

koma Iye adzakubatizani ndi Mzimu Woyera." Ndipo Yohane anali wotsimikiza kwambiri kuti Iye anali pa dziko lapansi, iye anati, "Iye ali pakati panu, penapake, tsopano."

49 Koma iye sankamudziwa Iye mpaka iye atawona chizindikiro icho chikutsikira pa Iye. Ndiye, pamene iye anawona Kuwala uko kukutsika pansi ndi kufalikira monga nkhunda, ndi kuwalira pa Iye, iye anati, "Ndi Uyo pamenepo. Ndi Ameneyo." Koma Yohane anali mmodzi yekhayo amene anawona Iko, inu mukudziwa. Yohane anali mmodzi yekhayo amene anamva Liwulo. Ena onse a iwo pamenepo, palibe amene analimva Ilo.

50 Koma ndiye pamene wantchito weniweni, woona abwerapo; ndi zonse zokopera kwa icho, ndi zakuti zidzasokoneze malingaliro a anthu. Satana amachita zimenezo. Ndipo iwo amene sangasiyanitse chabwino ndi choyipa, iwo amangogwera pamwamba pake. Koma Osankhidwa sadzachita zimenezo; Baibulo linati iye sadzakhoza kunyenga Osankhidwa. Ndipo tsopano, kusanachitike Kudza kwa Khristu, Baibulo linati, "Kukanadzakhala akhristu abodza akuwuka, ndipo akanadzadzinenera kuti ndi Khristu, ndipo akanadzati, 'Onani, anthu akuti Iye ali mchipululu.' Musati mukhulupirire zimenezo. 'Onani, Iye ali mchipinda chobisika.' Musati mukhulupirire zimenezo."

51 "Pakuti monga dzuwa limawalira kuchokera kummawa mpaka kumadzulo, chomwechonso kudzakhala Kudza kwa Mwana wa munthu." Mukuona? Inde, Iye adzatero—Iye adzatero—Iye adzawonekera, ndipo icho chidzakhala chinthu cha mdziko lonse. Ndipo tsopano icho chidza, tsopano, ndithudi, pamene iwo adzapeza kuti chinachake chachitika, mukuona, ndiye iwo adzati . . . Tsopano, kumbukirani, izo zidzachitika mwamsanga Mpingo utapita Kwawo, Mkwatulo utachitika.

52 Tsopano padzakhala kutsanzira kwabodza, nthawi zonse, ndipo ife sitikutanthauza kuti tilumikizane ndi chirichonse monga icho. Ayi, bwana.

53 Ndipo ine ndikukhulupirira kuti, pamene munthuyo adzabwera, uyu amene waneneredweratu kuti adzabwera, ine ndikusonyeza izo kokha mwa Malemba, kuti munthuyo adzayenera kukhala mneneri. Iye ndithudi adzakhala. Ndipo vumbulutso la Mulungu, chifukwa Mulungu . . . Mawu a Ambuye amadza kwa aneneri Ake. Ndiko kulondola ndendende. Ndizo . . . Ndipo Mulungu sangakhoze kusintha, mukuona. Ngati Iye akanati anali nako kachitidwe kabwinoko, Iye akanatero—Iye akanadzagwiritsa ntchito iko. Koma Iye—Iye ayenera . . . Iye anasankha kachitidwe kopambana kwambiri pachiyambi.

54 Monga ngati, Iye akanakhoza kusankha dzuwa kuti lidzilalikira Uthenga. Iye akanakhoza kusankha mwezi. Iye

akanakhoza kusankha a—mphepo. Koma Iye anasankha munthu. Ndipo Iye sanasankhe konse magulu. Anthu pawokha! Mukuona?

55 Ndipo sipanakhalepo konse aneneri awiri akuluakulu pa dziko lapansi pa nthawi yomweyo. Mukuona, munthu aliyense ndi wosiyana, iye amakhala nawo mapangidwe osiyana. Ngati Mulungu angakhoze kumupeza munthu mmodzi, ndizo zonse zomwe Iye ayenera kukhala nazo, mdzanja Lake momwe, Iye akhoza kuchita chimene Iye akufuna kuchita. Iye amangoyenera kukhala naye mmodzi basi. Mmasiku a Nowa; mmasiku a Eliya; masiku a Mose.

56 Ambiri anawuka, mu nthawi ya Mose. Inu mukudziwa momwe iwo anachitira, ndipo ankafuna kunena kuti, "Chabwino, sindiwe mmodzi yekhayo woyera mu gululi," ndipo—ndipo Datani ndi—ndi Korah.

57 Ndipo Mulungu anati, "Ingodzipatula wekha. Ine ndingotsegula nthaka ndi kuwameza iwo psyiti." Mukuona? Ndipo—ndipo kotero . . .

58 Ndiye kenako anthu anayamba kudandaula. Iye anati, "Ine ndingo—ine ndingochotsapo chinthu chonsechi."

59 Ndipo pamenepo Mose anatenga malo a Khristu, atatero, anadziponyera yekha pakati, ndipo anati, "Musachite zimenezo, Ambuye." Mukuona? Ndipo, ndithudi, iye . . . Atatha kumudzoza Mose kuti akachite ichi, Iye sanadze pa Mose, chifukwa iye anali akuchita monga Khristu mu nthawi imeneyo. Anali Khristu mwa Mose. Mwamtheradi.

60 Tsopano, ndife okondwa kwambiri lero kuti Mulungu akudziulula Yekha kwa ife. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Tsiku lopambanalo likungoyamba kumene kucha, likutulukira. Kuwala kukuyamba kung'anima. Mbalame za ku paradizo zikuyamba kuimba mu mtima wa oyera. Iwo akudziwa kuti si kale tsopano. Chinachake chichitika, chikungoyenera kutero. Kotero ngati "Iye samachita chirichonse . . . "

61 Tsopano, Malemba onse ndi odzozedwa. Malembawo ayenera mwamtheradi kukhala Choonadi. Palibe njira yowazungulira iwo. Apo ndi pamene ine ndimasiyana nawo abwenzi athu, mpingo wa Katolika. Ine ndimakhulupirira kuti Iwo sanangolembedwa ndi anthu wamba. Ine ndimakhulupirira kuti Iwo ankasunthidwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo zinthu zonse zazing'ono izi zomwe zawonjezeredwa, kuyesetsa kuwonjezera kwa Iwo; kodi inu munazindikira, mu kukonza, chirichonsecho chinachotsedwamo.

62 Ndipo Malemba enieni awa, owona amalumikizana, limodzi ndi limzake, mpaka umo—mulibemo kutsutsana mwa iwo, palibe kalikonse nkomwe. Ndiwonetseni ine chidutswa chimodzi cha zolembedwa chimene chingakhoze—chimene chingakhoze kulemba ndime, nkomwe, popanda kudzitsutsa chokha, kapena

kulemba—kulemba ndime, kapena ziwiri. Ndipo Baibulo silimadzitsutsa Lokha, paliponse. Ine ndamumvapo wotsutsa wakale akunena zimenezo, koma ine ndaperekapo mwayi kwa iye kwa nthawi yayitali, kuti andisonyeze ine pamene izo ziri. Izo siziri mkati umu. Izo zangokhala chomwecho chifukwa chakuti malingaliro aumunthu asokonezeka. Mulungu si wosokonezeka. Iye amadziwa chimene Iye akuchita. Iye amadziwa.

63 Taonani, ngati Mulungu ati adzaweruze dziko lapansi ndi mpingo, monga mpingo wa Katolika umanenera kuti ndi choncho, chabwino, ndiye mpingo wake ndi uti? Tangoyang'anani pa mipingo yomwe ife tiri nayo. Ife tiri nayo naini handiredi ndi chinachake, mabungwe osiyanasiyana a mipingo. Tsopano motani . . . Wina umaphunzitsa mwanjira *iyi*, ndi wina mwanjira *iyo*. Ndi chisokonezo bwanji, ndiye, aliyense akungochita chirichonse chimene iwo akufuna, inu mukumapitirirabe mulimonse. Mulungu ayenera kukhala ndi muyezo winawake, ndipo ndiwo Mawu Ake.

64 Ndikuyankhula . . . Osati kuponyera izo kwa Akatolika, tsopano, chifukwa a—Achiprotestanti ndi oyipa chimodzimodzi. Koma poyankhula ndi wansembe, iye anati, "Bambo Branham," iye anati, "Mulungu ali mu mpingo Wake."

65 Ine ndinati, "Bwana, Mulungu ali mu Mawu Ake. Ndipo Iye ndi Mawu." Inde, bwana.

Iye anati, "Chabwino, Iye ali . . . Mpingo ndi wosalephera."

66 Ine ndinati, "Iye samanena zimenezo. Koma Iye anati Mawu ndi osalephera."

67 Iye anati, "Chabwino, ife tinkaphunzitsa ubatizo umenewo mwanjira imeneyo, ndi zina zotero."

Ine ndinati, "Liti?"

Anati, "Mmbuyo mmasiku oyambirira."

Ine ndinati, "Kodi inu mumawulola uwo kukhala mpingo wa Katolika?"

Iye anati, "Inde."

68 Ine ndinati, "Ndiye, ndine Mkatolika, Mkatolika wachikale. Ine ndimakhulupirira mwanjira yachikale. Anthu inu lero mwawusokoneza Iwo wonse, ndipo palibe chirichonse mu Lemba chimene inu mumaphunzitsa. Kupembedzera ndi akazi ndi anthu akufa, ndi zinthu zina zonse izi, ndipo, oh, mai, kukhala osadya-nyama, ndipo, oh, ine sindikudziwa zina zonse, mukuona." Ine ndinati, "Inu mundipezere ine izo mu Lemba."

69 Iye anati, "Izo sizisowa kukhala mmenemo. Malingana ngati mpingo ukunena choncho, ndi zomwezo. Sizimapanga kusiyana kulikonse chimene Iwo akunena, ndi mpingo."

70 Ine ndinati, "Baibulo linanena, kuti, 'Aliyense amene adzawonjezere liwu limodzi kwa Ilo, kapena kuchotsamo

Limodzi, gawo lake lidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo.' Kotero, ndi Mawu! Ine ndimakhulupirira Mawu."

71 Tsopano, ndipo, ndiye, ngati Amosi akuti, ndi Malemba ena kuti apite nazo izo, kuti ngati. . .

72 Ndipo inu mukumbukire, pa ichi, kuti ife tikungokhudza nsonga zokha za Izo. Basi, mai, ngati. . .Pamene ine ndilowa mchipinda icho uko, ndipo—ndipo Kudzoza kumeneko kukabwera, ngati ndingakhoze kulemba zomwe Iye. . .zonse zomwe zimachitika, ine ndingakhale pano kwa miyezi itatu pa chimodzi cha Zisindikizozo. Kotero ndimangokhudza apo ndi apo ndi kungozipereka Izo, kokha zomwe zingawoneke kuti sizingawatsamwitse anthu. Koma, komabe, osati zokwanira kuwapweteka iwo, koma basi kungoti, pokhulupirira, kuti izo zikhoza—izo zikhoza kufotokoza chinthucho. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza.

73 Tsopano, penyani ichi tsopano, ngati "Mulungu samachita kanthu," anatero Amosi, "mpaka poyamba Iye atawulula icho kwa antchito Ake aneneri." Ndipo, ndiye, ife tikuwona chimene Iye akuchita. Izo zikuyenera kukhala kuti Iye akukonzekera kuchita chinachake, chimene Iye akuchiwulula tsopano. Mulungu akukonzekera kuti asunthire powonekera, mu chiweruzo, ine ndikukhulupirira. Iye akukonzekera kuti achite chinachake. Ndipo chinthu china kachiwiri, icho chikuchitira umboni ndithudi, kuti ife tiri mmasiku otsiriza. Ife tiri pa mapeto a m'badwo, M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya tsopano, pakuti zinthu izi zinali zoti zidzawululidwe kokha pa tsiku lotsiriza.

74 Tsopano, tangoganizani za izo tsopano. Tiyeni basi—tingoyesetsa kukhazikitsa mkati zomwe ife tikukhulupirira kuti Mzimu Woyera ukanatilola ife kuti tidziwe.

75 Tsopano kumbukirani, "Palibe choti chiwululidwe; Mulungu sadzachita kalikonse, ayi nkomwe, mpaka poyamba Iye atawulula kwa antchito Ake, aneneri." Ndipo Iye asanachite kalikonse, Iye amawulula icho. Ndipo pamene Iye awulula icho, inu mukhoza kukumbukira ichi, chinachake chiri pa njira yake. Mukuona, icho chikuwululidwa.

76 Ndipo zinthu izi zimene ife tikuzikamba zinali zoti zidzawululidwe pa tsiku lotsiriza, basi lisanafike Lipenga lotsiriza, pa mapeto pa Uthenga wa m'badwo wa mpingo wotsiriza. Uko nkulondola. Ngati mukufuna kuti muwerenge zimenezo tsopano, inu mukhoza kutsegula ku. . .Inu, ine ndinangolozera kwa inu, usiku wathawu, nthawi zitatu, Chivumbulutso 10:1-7, mwaona. "Ndipo mmasiku a kuwomba kwa Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, chinsinsi cha Mulungu chidzaululidwa ndi kudzatsirizidwa." Ndipo padzakhala chinthu chimodzi chokha chidzatsalire.

Pamene Bukhu losindikizidwa zisindikizo zisanu ndi ziwiri likutsegulidwa, ndiye chinsinsi chonse cha Mulungu. . .

77 Bwanji, ife tafufuza pa Izo, kudutsa mu zakazi. Ndipo molingana ndi Lemba, ndiye, ife. . .Panalibe njira yoti azimvetsere Izo mpaka tsiku lino, chifukwa Izo zakhala ziri zobisika. Ife tawona chophiphiritsa, chimene Icho chinaphiphiritsidwira nacho, koma Icho sichikanakhoza kuwululidwa molondola kufikira tsiku lotsiriza. Mukuona? Tsopano, ndiye, ife tiyenera kukhala pamenepo, pa—pa nthawi yotsiriza.

78 Tsopano, kumbukirani. Musati. . .Ndipo musaiwale tsopano, kuti, "Iye samachita kanthu mpaka Iye atawulula izo." Ndipo musaiwale, aponso, kuti Iye amachita izo mwanjira yophweka chomwecho, mwakuti, "Anzeru ndi aluntha amaziphonya izo." Tsopano, ngati mukufuna kuti mulembe zimenezo, ndizo Mateyu 11:25-26. Ndipo, kumbukirani, "Iye samachita kanthu mpaka Iye atachiwulula icho." Ndipo Iye amachiwulula icho mwanjira yakuti anthu anzeru, ophunzira amachiphonya icho. Kumbukirani, inali nzeru imene dziko linayikhumba mmalo mwa Mawu, pamene tchimo loyamba linachita zomwe ilo linachita. Musayiwale zimenezo tsopano. Oh, tiyenera kukhala oyamikira chotani, kuganiza za zimenezo!

79 Tsopano tangoyang'anani pa zinthu zimene zikuchitika! Yang'anani pa zinthu zomwe Iye watiuza ife! Yang'anani muno mu kachisi uyu, inu anthu amene takulira limodzi muno. Tsopano ine ndipempha matepi. . .Chabwino, kazipitirirani, zijambulani iwo. Koma, penyani, ine ndingoyankhula izi kwa anthu a mkachisiyu, inu amene mwakhala muli muno. Ine ndikulamulira aliyense wa inu, mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti muloze konse chala chanu pa chinthu chimodzi, mwa zinthu mahandiredi zomwe zinayankhulidwa izo zisanafike podzachitika, ndipo nenani kuti izo sizinachitike. Mundiuze ine nthawi imodzi, imene pa nsanja, kunja uko, kulikonse kumene kunali, imene Iye anayamba wayankhulapo chirichonse chimene sichinali mwangwiro ndendende basi mwanjira imeneyo. Motani? Angakhoze malingaliro a munthu kukhala mwanjira imeneyo? Ndithudi ayi.

80 Pamene Iye anawonekera kumusi uko pa mtsinje, zaka sartefirii zapitazo Juni akubwerayu, mmawonekedwe a Kuwala! Inu anthu akale mukukumbukira kuti ine ndinakuuzani inu, kuyambira ndiri mnyamata wamng'ono, Liwu lija ndi Kuwala kuja. Ndipo anthu ankaganiza, ndangokhala ngati ndasokonezeka mmutu pang'ono. Ndithudi, ine mwinamwake ndikanakhoza kulingalira chinthu chomwecho, winawake akananena zimenezo. Koma tsopano inu simukusowa kudabwa za Icho tsopano. Ndipo Mpingo sunadabwepo kuyambira 1933, kumusi ku mtsinje tsiku lija, kumene ine ndinali kubatiza mazana a anthu!

81 Ine ndikukumbukira kuti mnyamata wa Marra uja anandiuza ine, anati, "Inu mukupita kukawasambitsa anthu amenewo, Billy?" Jim Marra wamng'ono kumusi kuno, ine ndikuganiza kuti iye anafa tsopano. Ine ndikuganiza kuti iye anaphedwa kunja uko; mkazi wina anamuwombera iye. Koma iye—iye anandifunsa ine, "Kodi inu mukupita uko kukawasambitsa anthu amenewo?"

82 Ine ndinati, "Ayi, bwana. Ine ndikukawabatiza iwo mu Dzina la Ambuye wathu Yesu."

83 Ndipo apo panali mkazi akuyenda nawo mu gululo. Iye anati kwa mkazi wina, iye anati . . . anapanga ndemanga, chinachake chokhudzana ndi zimenezo. Iye anati, "Chabwino, ine sindingadandaule ndi kusambitsidwa." Anati, "Izo nzabwinobwino. Ine sindikusamala."

84 Ine ndinati, "Bwerera ndipo ukalape. Iwe siuli woyenera kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu." Mukuona?

85 Ichi si chinthu chosewera nacho. Uwu ndi Uthenga wa Khristu, wowululidwa mwa kutumidwa, Mawu. Basi, tsopano, ngati inu mukunena kuti, "Zamkutu ndi zopusa," inu mukanakhoza kuziyika izo penapakenso. Koma, kumbukirani, izo zinalonjezedwa mu Mawu kuti zikanadzachitika, ndipo ndendende basi momwe izo zikanadzakhalira. Ndipo apa izo ziri.

86 Ndiye, kumusi uko tsiku lija, pamene iwo anali ataimirira pa mtsinjepo! Ndipo Mngelo wa Ambuye, yemwe ine ndinakuuzani inu kuti Iye ankawoneka ngati a—nyenyezi kapena chinachake cha patali, kenako Icho chinafika pafupi, ndipo ndinakuuzani inu momwe Kuwala kwa emarodi kumawonekera. Ndipo apo Iko kunabwera, kunadzatsika pa mtsinje kumene pamene ine ndinali kubatiza.

87 Pamene, amuna amalonda kumusi kuno mu mzinda, anati, "Kodi icho chimatanthauza chiyani?"

88 Ine ndinati, "Icho sichinali cha ine. Icho chinali cha inu. Ine ndikukhulupirira. Mukuona? Icho chinali cha kwa inu, chifukwa chimene Mulungu anachitira icho, kukulolani inu kuti mudziwe kuti ine ndikukuuzani inu Choonadi." Pokhala kamwana, mnyamata, monga, ndipo pafupifupi usinkhu wa zaka twente-wani zakubadwa, iwo—iwo sakanakhoza kukhulupirira zimenezo, mukuona, chifukwa ndi zomuchulukira kwambiri mwana. Ndiyeno ine ndinali kuganiza . . .

89 M'bale Roberson pano, mmodzi wa matrastii athu, ine ndinamuwona iye pano maminiti pang'ono apitawo. Iye anali kundiuza ine tsiku lina za kukhala mu Houston pamene chithunzicho uko chinajambulidwa, chimene inu mumachiwona. Ndipo ine ndinali . . . Pa mtsutsano uja, ine ndinayamba kuyankhula chinachake chokhudza izo, usiku wina. M'bale Roy anali yekhayo . . . ndi munthu mmodzi wina, anali munthu

yekhayo mu gululo amene anali nacho chojambulira. Icho chinali chimodzi cha zojambulira zamawaya zachikale izo. Ine ndikumuwona M'bale Roberson tsopano, ndi mkazi wake. Kotero, ndipo—ndipo awa, Akazi a Roberson anali akudwala.

90 M'bale Roy anali msilikali wakale. Ndipo miyendo yake itawombeledwa, ndipo iwo anamugoneka iye panja kuti wafa. Iye anali ofesala mu—mu gulu Lankhondo. Ndipo Germany 88 inawombera kasinja uyu amene anali ndi iye, ndipo iyo inangomupha munthuyo, ndi kumuphulitsa iye mzidutswa. Iwo anamugoneka iye kumeneko, kuti wafa, kwa nthawi yaitali. Ndipo iwo anati iye sakanadzayendanso konse, chifukwa miyendo iwiri yonse inali itaphwanyika, mitsempha mwa iyo, ndi zinthu. Mai, iye akhoza pafupifupi kundiposa ine kuyenda.

91 Koma chinali chiyani chimenecho? Panali chinachake chimene iye anachiwona, ndipo anapita ku Houston. Ndipo anali kundiuza ine za mkazi wake. Ndipo iye ali ndi—iye ali ndi waya; amumangirira iye pa tepi. Ndipo misonkhanoyi ikatha pano, chabwino, iye adzakumvetseretsani inu nonse zimenezo, ine ndikudalira. Ndipo pa tepi yakale ya waya uko, iye ali nawo mauthenga anga olalikidwa mu Houston. Ndiyeno mkazi wake, iye anati, anajambula iyo kumeneko, ndipo iye sanazindikire izo kufikira tsiku lina.

92 Mkaziyo anali, oh, iye anali wachisoni kwambiri. Iye anali akudwala, ndipo iye ankafuna kulowa mu mzere wa pemphero. Iwo sankandidziwa konse ine, ndipo ine ndinali ndisanawawonepo iwo mmoyo wanga. Kotero iye anali atakhala pa a—zenera tsiku limenelo, akuyang'ana panja, ndipo ali wokhumudwa kwambiri, inu mukudziwa, ndi wosokonezeka, ndipo akukhumba akanakhoza kupeza khadi la pemphero, kuti akhale mu mzere.

93 Ndipo, zinachitika kuti, usiku umenewo iye anakhala mu mzere, kapena usiku winawo, kapena chinachake. Ine ndikukhulupirira, usiku womwewo. Ndipo iye analowa mu mzere. Ndipo pamene iye anafika pa nsanja, Mzimu Woyera unamuuza iye, unati, "Tsopano, iwe siuli wochokera kuno. Iwe ndi wochokera ku mzinda wotchedwa New Albany." Ndipo unati, "Iwe unali utakhala pa zenera lero, ukuyang'ana kunja, ndipo ukudandaula za kupeza khadi la pemphero." Izo ziri pamenepo, pa tepi, zaka zapitazo.

94 Ndiyeno pa mayambiriro a msonkhanowo, pamene Mzimu Woyera unali pamenepo . . . Uwo unali woyamba wa msonkhanowo. Ife tinali nawo pafupifupi anthu firii sauzande okha, kenako ife tinafika mpaka eyiti sauzande, kenako mpaka pafupifupi sarte sauzande. Kotero ndiye mu . . . Pamene ine ndinali kuyankhula pa . . . Umodzi wa misonkhano yoyambirira imene, ine ndinati, "Ine sindikudziwa chifukwa chimene ine ndikunenera izi." Tsopano, izo ziri pa tepi. "Koma, ndizo, ife

tiri. . . Iyi ikhala imodzi mwa nthawi zanga zapamwamba. Chinachake chichitika mu msonkhano uno, chomwe chikhale chopambana kwambiri kuposa chomwe aliyense anachiwonapo konse."

95 Ndipo awo anali chabe pafupifupi eyiti kapena naini, mausiku teni zitachitika zimenezo, pamene Mngelo wa Ambuye anadzawonekera pamaso pa pafupifupi anthu sarte sauzande, ndipo anabwera kumeneko, ndipo chithunzicho chinajambulidwa. Ndi Icho apo, pakali pano, chomwe chinakoperedwa mu Washington, DC, monga Chinthu chauzimu chokhacho chimene chinajambulidwapo mdziko lapansi.

96 Ndiye ine ndinayankhula za, inu mukudziwa, kuzinena izo nthawizina, pansi pa kuzindikira zamumtima, kuti, "Munthu waphimbidwa ndi mthunzi wa imfa. Apo pali chophimba chakuda, cha mthunzi. Iwo akuyembekezera kufa."

97 Ndiyeno cha kuno ku East Pines, kapena Southern Pines, ine ndikukhulupirira ndi kumeneko, basi pamene ine ndinali kumeneko mu msonkhano wotsiriza. Dona wamng'ono atakhala pamenepo, ndipo Chinachake chinamuuza iye, "Jambula chithunzi chimenecho, mwamsanga pamenepo," pamene ine ndinali kuyankhula kwa dona. Ndipo icho chinali pamenepo. Ine ndikuganiza kuti chikhala chiri pa bolodi la zolengeza; chakhala chiripo, kwa kanthawi ndithu. Ndi chimenecho chophimba chakudacho chitapachikika pa donayo pomwepo.

98 Iye anajambula chithunzi china, mwamsanga pamene Mzimu Woyera unalengeza izo. Icho chinali chitachokapo. Unati, "Iwe uchiritsidwa. Ambuye akuchiza iwe. Khansayo yachokapo." Ndipo izo zinali pamenepo. Ndipo iye anachiritsidwa. Mukuona? Ndi zimenezotu. Mukuona?

99 Izo zimangosonyeza kuti Mulungu amadziwa yomwe ili nthawi ya tsiku. Ife sitimadziwa. Ife timangoyenera kumamumvera Iye.

100 Tsopano ife tikhoza kumangoyankhulabe, koma tiyeni titsikire apa tsopano, miniti yokha, ndipo tikhudze Chisindikizo cham'mbuyo ichi, kuchitira kuti ife tikhoze kulumikizitsa izi kwa Icho. Tsopano, kungobwereza chabe, kwa mphindi pang'o-. . . mphindi pang'ono, chi—chinacho, Chisindikizo Choyamba.

101 Ife tikuzindikira, mu kumatula kwa Chisindikizo Choyamba, Satana ali naye—munthu wapamwamba, wachipembedzo. Kodi inu munamuzindikira wokwera pakavalo-woyera uja? Amene, iwo, iye ankaganiziridwa kuti anali. . . Mpingo woyambirira ukutulukira; koma, oh, mai, izo zakhala zikuphunzitsidwa kudutsa mu zaka, koma izo sizikanakhoza kukhala chomwecho. Inu mudzangoyang'ana pamene ena onsewo, pamene ife tidzawamangirira iwo onse limodzi, ndiye mudzayang'ane pamene izo ziri, mwaona.

Tsopano, ndipo ine sindikudziwa chimene ena onsewo ati adzakhale, panobe. Koma ine ndikudziwa kuti izo ziyenera kubwera mwangwiro basi mmenemo, chifukwa ndicho Choonadi. Icho ndi Choonadi. Umenewo unali utsogoleri wolowezana wa mpingo waku Roma, ndendende.

102 Anthu awa amene amaganiza kuti Ayuda ndi otsutsakhristu, iwo ndithudi achoka pa mzere mamailosi millioni. Inu musadzaganize konse kuti Ayuda ndi otsutsakhristu. Maso awo anachititsidwa khungu, ndicholinga, kuti ife tidzakhoze kukhala nayo njira yolowera mkati, kutipatsa ife nthawi ya kulapa.

103 Koma wotsutsakhristu ndi Wamitundu. Ndithudi. Iye ndi wokopera wa Choonadi; *anti*, "kutsutsa." Tsopano, munthu wamkulu wapamwamba uyu, oh, momwe iye anadzakhalira munthu wopambana, ndipo—ndiye kenako potsiriza anadzapatsidwa mpandowachifumu. Ndiyeno, atatha kupatsidwa mpandowachifumu, iye anavekedwa korona. Ndipo tsopano, iye, zitatha izo, iye anali kupembedzedwa mmalo mwa Mulungu.

104 Tsopano, taonani, izo zisanabwere konse. Ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake. Anali ndani ameneyo? Kodi Icho chinali chiyani pa Paulo, mu Atesalonika Wachiwiri 2:3, amene anati munthu ameneyo akanadzabwera? Ndi chifukwa chiyani munthu ameneyo anayang'ana mmusi kudutsa m'badwo ndi kuziwona izo? Iye anali mneneri wa Mulungu. Ndithudi. Chifukwa chiyani . . .

105 Iye anati, "Mzimu ukuyankhula momveka, kuti m'masiku otsiriza iwo akanadzachoka ku chikhulupiriro, ndipo akanadzamvetsera ku zodolola . . ." Inu mukudziwa kuti *kudolola* ndi chiyani. Mzimu wodolola mu mpingo, awo ndi atumiki. "Kudolola, mzimu wa atumiki, machitidwe a ziwanda; zinyengo mu mpingo."

106 "Ammutu, amalingaliro apamwamba," nzeru, inu mukuona, anzeru, aluntha; "okhala nawo mawonekedwe a umulungu." (Kumangopita, nkumati, "Chabwino, ndife Akhristu; ife tiyenera kumapita ku tchalitchi.") "Kukhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana mavumbulutso, Mphamvu ndi kugwira ntchito kwa Mzimu; kwa oterewo chokaniko." Mukuona? Tsopano zindikirani, iye anati, "Pakuti awa ndi mtundu umene uti udzapite nyumba ndi nyumba, ndipo adzatsogolera akazi opusa . . ." Izo sizikutanthauza akazi a Mzimu Woyera. "Akazi opusa otengeka nako kusilira kosiyanasiyana."

107 Kusilira kosiyanasiyana! Iwo amangokonda kulowerera mu kanthu kalikonse kakang'ono kamene iwo angakhoze kulowamo, ndi mitundu yonse ya magulu; ndi kumakhala mulimonse momwe iwo akufunira kutero, ndipo, komabe,

"Ife timapita ku tchalitchi. Ife tiri basi abwino monga aliyense." Zovina, maphwando, kumadula tsitsi lawo, kudzipaka penti, kumavala chirichonse chimene iwo akufuna; komabe, "Ndife—ndife Achipentekoste. Ndife—ndife basi abwino monga aliyense." Oh! Ntchito zanu zomwe zikukuzindikiritsani inu. Zoona. Zindikirani.

108 Koma iye anati, "Anthu amalingaliro osokonekera, pa Choonadi." Kodi Choonadi ndi chiyani? Mawu, amene ali Khristu. "Pa Choonadi."

109 "Oh, iwe umapanga . . . Iwe, ndiwe wothamangitsa-akazi. Ndiwe wodana ndi akazi. Umachita *izi*, *izo*."

110 Ayi, bwana. Izo sizoona. Ndiro bo—bodza. Ine sindimadana ndi akazi. Ayi, bwana. Iwo ndi alongo anga, ngati iwo ali alongo. Koma chinthu chimene ine . . .

111 Chikondi chimakonza. Ngati icho sichikukonza, icho si chikondi. Ngati icho chiri, ndiye, ngati chiri chikondi, ndi—ndi chikondi cha phileo ndipo osati agapao, ine ndikukuuzani inu zimenezo. Iwo akhoza kukhala nako kachikondi pang'ono ka phileo kwa dona wina wa mawonekedwe abwino. Koma chikondi cha agapao ndi chinthu chosiyana, ndicho chikondi chimene chimawongola chinthucho, ndi kukakumana naye Mulungu kutsidya kwinakwake kumene ife tikhoza kukakhala Kwamuyaya. Mukuona? Ine sindimatanthauza zimenezo, mwinamwake, momwe izo zinamvekera, koma ine . . . Inu mukudziwa chimene ine—ine . . . Ine ndikuyembekeza kuti inu mukumvetsa. Chabwino.

112 Tsopano, koma, kumbukirani, iye anati, "Monga Ayane ndi Ayambre anamutsutsa Mose, momwemonso adzatero iwo. Koma kupusa kwawo posakhalitsa kunawonekera."

113 Chifukwa chiyani? Pamene Mose anatumidwa kukachita chinachake chimene chinkawoneka chopusa, koma, iye anapita kumeneko moona mtima basi momwe iye akanakhoza kukhalira. Ndipo Mulungu anamuuza iye kuti atenge iyi, ndodo iyi, ndi kuti akayiponyere iyo pansi, ndipo iyo inasanduka njoka. Ndiye, Iye anachita zimenezo, kuti amuwonetse iye chimene chikanadzachitika. Ndipo pamaso pa Farao, iye anaimirira kumeneko basi monga momwe Mulungu anamutumira iye, ndipo anaponyera pansi ndodo yake, ndipo iyo inasanduka njoka.

114 Ndipo mosakayika, Farao anati, "Ndale ya matsenga otchipa!" Kotero iye anapita ndipo anakatenga Ayane ndi Ayambre ake. Anati, "Ife tikhoza kuchita zinthu zimenezo, nafenso." Ndipo iye anaponyera pansi ndodo, ndipo izo zinasanduka njoka.

Tsopano kodi Mose akanakhoza kuchita chiyani?

115 Chinali chiyani chimenecho? Uko kunali kuwonetsera kuti, chinthu chenicheni chirichonse cha Mulungu, mdierekezi

amakhala naye wotsanzira wa icho. Iwo amatsanzira, kuti awaponyere anthu kunja kwa njirayo.

116 Kodi Mose anachita chiyani, anati, "Chabwino, ndikuganiza ndalakwitsa. Ine kulibwino ndibwerere"? Iye anangoyima njii, pakuti iye anali atachita utumiki wake, mpaka ku lemba.

117 Kenako, chinthu choyamba inu mukudziwa, njoka ya Mose inadya zinazo. Mukuona? Kodi inu munayamba mwaganizapo za chimene chinachitika kwa njoka zinazo? Izo zinapita kuti? Mose ananyamula ndodoyo ndipo anatuluka nayo iyo. Iye ankachita zozizwitsa nayo iyo. Ndipo njoka izo zinali mkati mwa ndodo ina iyi. Mukuona? Ndicho chodabwitsa. Sichoncho icho? Inde, bwana.

118 Tsopano, wotsutsakhristu akubwera mu kuwala, mwa pang'onopang'ono. Ine ndikufuna kuti inu muzindikire ichi. Tsopano, pamene inu mumva . . .

119 Tsopano, kwa amzanga Achikatolika, ingokhalani chete miniti yokha, ndipo tsopano; ndiyeno ife tiwona pamene Achiprotestanti; pamene ife tonse tiri, mukuona.

120 Zindikirani, mpingo woyamba, pamene mpingo wa Katolika unena kuti iwo anali oyamba, mpingo wapachiyambi, iwo akulondola ndendende. Iwo anali. Iwo anayambira pa Pentekoste. Apo ndi pamene mpingo wa Katolika unayambira. Tsopano, ine nthawi ina sindinkakhulupirira nkomwe zimenezo, mpaka ine nditawerenga mbiriyakale, ndipo ine ndinapeza kuti izo nzolondola. Iwo anayambira pa Pentekoste. Koma iwo anayamba kulowerera, ndipo inu mukuona pamene iwo ali.

121 Ndipo ngati Pentekoste izilowerera ndi liwiro limene iyo ikulowerera tsopano, iwo sadzasowa kupita zaka thuu sauzande. Mu zaka handiredi kuchokera tsopano, iwo adzakhala kutali kwambiri kuposa momwe mpingo wa Katolika uliri. Izo nzoona.

122 Koma zindikirani, momwe, wokwera pakavalo woyera uyu. Tsopano ife tingoyika maziko a zimenezo, pang'ono, mpaka tigunde Chisindikizo ichi. Tsopano zindikirani wokwera pa kavalo woyera, pamene iye anatulukira, iye—iye akutumikira mmagawo atatu. Mdierekezi, monga ndinatsimikizirira kwa inu usiku wina, ali mu utatu, chimodzimodzi ngati Mulungu. Koma ndi mdierekezi yemweyo nthawi zonse, mmagawo atatu. Zindikirani magawo ake. Mu gawo loyamba, iye anabwera mmenemo . . .

123 Mzimu Woyera unagwa, ndipo anthu anali nazo zonse mofanana. Ndipo Mzimu wa Mulungu unali pa iwo. Ndipo atumwi ankapita nyumba ndi nyumba, akunyema nawo mkate anthu. Ndipo kunali zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa zikuchitidwa.

124 Ndipo—ndipo kenako, chinthu choyamba inu mukudziwa, Satana anayamba kupangitsa kuti kung'ung'udza kubwerepo.

125 Kenako, patapita kanthawi, akapolo awa ndi osauka a mdzikolo, amene analandira Mzimu Woyera, iwo ankapita ku malo osiyanasiyana, akuchitira umboni. Iwo ankachitira umboni kwa mabwana awo.

126 Ndipo patapita kanthawi, panayamba kubwera, oh, monga akapitao ankhondo ndi—ndi anthu osiyanasiyana. Otchukawo anayamba kuwona kuchirimikako, ndi zozizwitsa ndi zizindikiro zomwe amuna awa ankachita, zitatero iwo anavomereza Chikhristu.

127 Chabwino, ndiye, inu mukuona, pamene iye anakumbatira Chikhristu, ndi kutsikira kumeneko ku malo amene iwo ankasonkhana, mu holo yaing'ono, yakale yamdima ya ndowe; ndipo nkumawomba mmanja, ndi kumafuula, ndi kumayankhula mmalirime, ndi kumalandira mauthenga. Bwanji, iye sakanakhoza konse kuzitengera izo kwa wake—wopikisana naye, kapena chirichonse chimene chiri, mu geni yake. "Iye sakanakhoza konse kukhulupirira Zimenezo, monga chomwecho." Ndithudi ayi. Kotero, iye ankayenera kuchiveka Icho. Kotero iwo anayamba kusonkhana pamodzi, ndipo anayamba kulingalira, "Tsopano ife tipanga chinachake chosiyanako pang'ono."

128 Ndipo Yesu, pomwepo mwamsanga, pa m'badwo wa mpingo woyamba, Iye anawauza iwo. Mu mutu wachiwiri wa Chivumbulutso apa, "Ine ndiri nacho chinachake chokutsutsa iwe, chifukwa cha ntchito izi za Chinikolai."

129 *Nikao*, "kugonjetsa" anthu wamba. Mwa kuyankhula kwina, iwo ankafuna kupanga, mmalo mwa aliyense kukhala mmodzi, iwo ankafuna kumupanga munthu wina woyera. Iwo ankafuna kupanga china cha mtundu wa . . . Iwo ankafuna kuchifanizitsa icho ndi zachikunja, mofanana ndi kumene iwo anachokerako, ndipo iwo potsiriza anachita zimenezo.

130 Tsopano penyani. Poyamba, "Chinikolai." *Chinikolai* chinali kutchedwa, mu Baibulo, "wotsutsakhristu," chifukwa icho chinali kutsutsana ndi Chiphunzitso chapachiyambi cha Khristu ndi atumwi.

131 Ine sindikufuna kutchula dzina la munthu uyu. Iye ndi munthu wotchuka. Koma ine ndinali pa msonkhano wake, kuno zaka zingapo zapitazo. Ndipo iye anadziwa kuti ine ndinali pamenepo, chifukwa ine ndinali nditagwirana naye chanza. Ndipo iye anati, "Oh, inu mukudziwa, ife tiri nawo otero lero amene akuwatcha Achipentekoste." Ndipo iye anati, "Iwo, iwo amadalira pa Bukhu la Machitidwe." Ndipo iye anati, "Inu mukuona, Machitidwe inali ntchito ya miyanga chabe kwa Mpingo."

132 Inu mungakhoze kulingalira, munthu amene anawerenga Baibulo, munthu wochirimika wakale, ndipo anali atawerenga Baibulo mwanjira yomwe bambo uyo anachitira, ndiyeno

nkupanga ndemanga yonga imeneyo? Izo zinamveka, izo sizi . . . Izo—izo sizikumveka ngati Mzimu Woyera nkomwe. Chabwino, izo sizikuyenera kutero, kulikonseko.

133 Chifukwa, aliyense wakamvedwe kawamba akanakhoza kudziwa kuti Machitidwe a Atumwi sanali machitidwe a atumwi. Iwo anali machitidwe a Mzimu Woyera mwa atumwi. Kodi inu simukudziwa momwe ife tinazifanizira izo mmibadwo ya mpingo? Zamoyo izo zitakhala pamenepo, zikuyang'anira Likasa ilo pamenepo. Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, atayima pamenepo, akulondera Ilo. Ndipo mwa Ilo muli zimene zinachitika, monga zotsatira za zolemba za Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane.

134 Ndi chimene mtengowo unatulutsa . . . nthambi yake yoyamba, ndipo ndizo zimene zinachitika. Ndipo ngati mtengo umenewo udzatulutse konse nthambi ina, iwo adzalemba Bukhu lina la Machitidwe pambuyo pa iyo. Chifukwa, inu mukuona, Moyo womwewo uyenera kukhala mwa chinthu chomwecho.

135 Chotero tsopano, lero, pamene ife tiyang'ana pa mipingo yathu ya chipembedzo, Methodisti, Baptisti, Presbateria, Lutherani, Mpingo wa Khristu (wotchedwa chomwecho), ndi Achipentekoste ndi zinthu, kodi ife timazipeza kuti zimenezo? Inu simumazipeza izo.

136 Ine ndivomereza kuti Achipentekoste ali nacho chinthu chapafupi kwambiri kwa Icho, chimene chiripo, chifukwa iwo ali muno mu M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Iwo anali nacho Choonadi ndipo anachikana Icho. Iwo anafunda nacho Icho, ndipo Mulungu anawalavula iwo kuchokera mkamwa Mwake. Ndizo ndendende molingana ndi Malemba.

137 Inu simungawapangitse Malemba amenewo kunama. Mukuona? Iwo adzakhala owona, nthawizonse. Musamayesere kutero . . . Chinthu chokhacho, musamayesere kufoletsa lingaliro lanu kwa . . . kapena Malemba kufola molingana ndi lingaliro lanu. Koma ku- . . . muzidzifoletsa nokha ndi Malemba. Ndicho, mukatero mukuyenda ndi Mulungu. Ziribe kanthu ndi zochuluka bwanji zomwe inu mukuyenera kudulapo, kapena kuziyika pambali, muzidzifoletsa ndi Iwo. Mukuona?

138 Taonani chimene Iwo anachita nthawi yoyamba imene Iwo anagwa. Chabwino, ngati Mulungu anachita monga chomwecho nthawi yoyamba, Iye ayenera kuchita chomwecho nthawi yachiwiri. Iye ayenera kuti azichita monga chomwecho nthawi iliyonse, kapena Iye anachita molakwika nthawi yoyamba.

Mwaona, ife monga anthu achivundi, ife tikhoza kulakwitsa. Mulungu sangakhoze kutero.

139 Lingaliro loyamba la Mulungu ndi langwiro. Ndipo momwe Iye anasankhira kuchita zinthu, sipangakhalenso njira ina, yabwinoko. Iye sangatukuke pa iyo, chifukwa iyo ndi yangwiro, kuyamba ndi kuyamba. Ngati si choncho, ndiye Iye

si wopandamalire. Ndipo ngati Iye ali wopandamalire, ndiye Iye ndi wodziwazonse. Ndiye ngati Iye ali wodziwazonse, Iye ali wamphamvuzonse. Ameni! Iye ayenera kukhala chimenecho, kuti akhale Mulungu. Mukuona? Kotero inu—inu simunganene kuti, tsopano, "Iye anaphunzira mowonjezera." Iye sanaphunzire mowonjezera, Iye ali—Iye ndi kasupe kumene wa nzeru zonse. Mukuona?

140 Nzeru zathu kuno zimachokera kwa Satana. Ife tinazitengera izo kuchokera ku Edeni, kumene tinasinthanitsa chikhulupiriro pofuna nzeru. Eva anachita zimenezo.

141 Tsopano, iye poyamba ankatchedwa wotsutsakhristu. Gawo lachiwiri, iye ankatchedwa mneneri wabodza, chifukwa mzimu umenewo pakati pa anthu unadzakhala mu thupi.

142 Inu mukukumbukira, wokwera pa kavalo woyera tsopano analibe korona pamene iye ankayamba, koma kenako iye anadza . . . anadzapatsidwa korona. Chifukwa chiyani? Iye anali mzimu wa Chinikolai, kuyamba ndi kuyamba; ndipo kenako iye anadzakhala mu thupi mwa munthu; ndipo zitatero iye anavekedwa korona, ndipo analandira mpandowachifumu ndipo anavekedwa korona. Ndipo kenako iye anatumikira apo kwa nthawi yaitali, monga momwe ife tiwonere pamene ife . . . Zisindikizo zikumatulidwa.

143 Ndiyeno ife tikupeza kuti, patapita nthawi yaitali imeneyo, Satana anathamangitsidwa Kumwamba. Ndipo iye anabwera pansi, molingana ndi Malemba, ndipo anadzaziyika yekha pa mpandowachifumu. Tangoganizani, anadzaziyika yekha pampandowachifumu mwa munthu ameneyo, ndipo anadzakhala chirombo. Ndipo anali nayo mphamvu, mphamvu yapamwamba, ndi zimenezo iye ankachita, zozizwitsa zonse ndi chirichonse, chimene—chimene, kapena kuphana ndi kumenyana kwamagazi ndi chirichonse chimene—chimene Roma akanakhoza kuchita. Chabwino. Iye ankapha mwa nkhanza, chilango cha Chiroma. Basi, oh, momwe ife tingakhoze kulowa mu Malemba ena apa!

144 Kumbukirani, Yesu Khristu anafa pansi pa chilango cha Roma, chilango cha imfa.

145 Uthenga umene ine ndiri nawo mu mtima mwanga, kuti ndilalikire pano pa msonkhano wotsatira uwu, pa Lachisanu la Isitara masana, pakukumana zitatu, zinthu foro, mukuona. "Kumeneko iwo anamupachika Iye." "*Kumeneko*," malo oyeretsetsa, achipembedzo padziko lapansi anali Yerusalemu. "*Iwo*," anthu oyera kwambiri (oganiziridwa kuti anali) mdziko, Ayuda. "Kumeneko iwo *anamupachika*," chilango chankhanza kwambiri chimene Roma akanapereka. "Anamupachika *Iye*." Chiyani? Munthu wamkulu kwambiri amene anayamba wakhalapo ndi moyo. "Kumeneko iwo anamupachika Iye." Oh, mai!

146 Mulungu andithandize ine kuti ndikachizunguze Icho mu gulu ilo la anthu amalonda, mpaka iwo akakhoze kuwona pamene iwo akuyima. Chabwino. Tsopano, osati kuti ndikhale wosiyana, osati kuti ndikhale woyipa; koma kuti ndikachigwedeze Icho, mpaka abale awo akakhoze kuwona kuti olemekezeka awo ndi atate oyera awo, ndi zinthu zomwe iwo akulemba mu bukhu ili la Amuna Amalonda, ndi zamkutu. Akhristu sayenera kumamutcha munthu aliyense "Atate." Iwo anayambira kumbuyo, ine ndayesetsa kuwathandiza iwo mu chirichonse chimene ine ndingakhoze (Inu mukuona tsopano kumene tepi iyi ikupita.), kotero, ine ndamaliza, Ine ndithudi sindidzakhala nacho chochita china chirichonse ndi izo. Chabwino. Poyamba, kumbukirani Khristu.

147 Poyamba, monga Chiniko-. . . Chinikolai, ndipo kodi m'badwo wa Chinikolai unapempha chiyani? Iwo unapempha kuti uchoke ku gulu la anthu awo amene amafuula ndi kumawomba mmanja, ndi kumawoneka ngati zamanyazi; monga iwo anachitira pa Pentekoste, kumachita ngati anthu oledzera, akudzandima mu Mzimu, ndi zinthu. Iwo sanafune chirichonse cha zinthu zimenezo. Iwo anati iwo anali ataledzera. Ndipo pamene otchuka. . . Mvetserani! Musaphonye izi. Izo zikhoza kumveka mwa misala kwa inu, koma ndicho Choonadi. Pamene o—olemekezeka anayamba kulowamo, iwo sakanakhoza kudzitsitsa kwa izo.

148 Nchiyani chimamupangitsa Mulungu kukhala wamkulu, ndi chifukwa chakuti Iye ndi wamkulu mokwanira kudzitsitsa pansi. Ndicho chimene chimamupangitsa Iye kukhala wamkulu. Palibe chinthu china chachikulu kwambiri. Ndipo Iye anadzitsitsa mmusi kwambiri mwakuti palibe akanakhoza kudzitsitsa chomwecho, munthu aliyense anayamba wadzitsitsapo konse. Iye anali Mfumu ya Kumwamba, ndipo Iye anabwera ku—ku mzinda wotsikitsitsa padziko lapansi, Yeriko. Ndipo Iye anadzitsitsa kwambiri mpaka ngakhale munthu wamfupi kwambiri mu tawunimo ankachita kuyang'ana pansi pa Iye, kuti amuwone Iye. Nkulondola uko? Zakeyu. Uko nkulondola. Iye ankatchedwa dzina loyipitsitsa limene munthu aliyense angakhoze kutchedwa, "wamatsenga, mdierekezi, Belezebule." Ndicho chimene dziko linkaganiza za Iye. Anafa imfa yankhaza kwambiri. Analibe malo woti agonekepo mutu Wake. Anakankhidwa kunja, ndi bungwe lirilonse.

149 Koma pamene Mulungu anamukweza Iye, pamwamba kwambiri mpaka Iye amayenera kuyang'ana pansi kuti awone Kumwamba. Mukuona momwe, Mulungu, aliri mu kudzichepetsa. Mukuona? Ndipo Iye anamupatsa Iye Dzina lalikulu chotero mwakuti banja lonse la Kumwamba limatchedwa ndi dzina Lake, ndi banja lirilonse la pa—pa dziko lapansi. Banja lonse padziko lapansi limatchedwa "Yesu." Mabanja onse a Kumwamba amatchedwa "Yesu." Ndipo Dzina

loterolo, limene, bondo lirilonse lidzagwada, ndipo lirime lirilonse lidzavomereza, kwa Iye kukhala Ambuye; kuno kapena mu gehena. Gehena idzagwadira kwa ilo. China chirichonse chidzagwadira kwa ilo. Mukuona? Koma poyamba kunali kudzichepetsa, kenako ilo linadzakhala lalikulu. Mukuona? Muloleni Mulungu akukwezeni. "Iye amene adzichepetsa yekha, Mulungu adzamukweza." Mukuona?

150 Tsopano, ife tikuzindikira kuti mzimu wa *nikao* uwu unkafuna nzeru, ophunzira kwambiri. Iwo unkachita kulingalira izo, monga zinachitikira mu Edeni, kulingalira motsutsa Mawu a Mulungu, mwa nzeru, ndipo mpingo unagwera zimenezo. Chinali chiyani chimenecho?

151 Tsopano, tiyeni tinene kuti, tiwutenge mpingo uwu pano, ndipo titenge gulu la anthu monga ife tilirimu, ngati inu simunali odzazidwa-Mzimu kwenikweni. Ndipo tiyeni titenge, titi . . . Tsopano, palibe chirichonse chowatsutsa ameya a mzinda wathu. Ine sindikuganiza kuti ine ndikuwadziwa iwo, Bambo Bottorff. Kodi iwo akanalibe ameya? Bambo. . . . ine sindiri . . . Mukuona? Ine sindiri . . . Bambo Bottorff ndi bwenzi wabwino wa ine, mwaona. Koma, tingoti, meya wa mzindawu, ndi apolisi onse, ndi—ndi akapitawo onse, ndipo iwo—iwo onse amabwera kuno. Chinthu choyamba inu mukudziwa, ngati iwo ali ndi kanthu kakang'ono chabe m'mutu mwawo, ndipo ndikuyamba kuyankhula kwa gulu la atsogoleri ndi anthu ozungulira pano, ndi kuti, "Tsopano inu mukudziwa chiyani? Izi ziyenera kukhala zosiyana." Ngati inu simuli odzazidwa-Mzimu, ndi kukhala naye mwamuna wodzazidwa-Mzimu kuseri kwa guwa, chinthu choyamba inu mukudziwa, inu muyamba kugonjera kwa iwo. Mwinamwake osati m'badwo uno; mwina m'badwo wotsatira.

152 Ndipo ndi momwe izo zinayambira mmenemo. Mukuona? Chifukwa chiyani? Iwo ankati, "Tayang'anani apa. Izo ndi zomveka." Inu, inu ndikumamvetsera.

153 Tinene kuti munthu kulowa mkati muno, amene anganene kuti, "Tchalitchi chino ndi chaching'ono kwambiri. Tiyeni timange tchalitchi chachikulu. Ine ndikumangirani inu china pano, icho ndi . . . icho chidzakhala cha ndalama zochuluka kwambiri, theka la madola millioni. Izo zidzaikidwa mmenemo. Ine ndidzachiyika chinthucho pa wayilesi." Pamene iwo achita zimenezo, ndiye kuti ali ndi nkhwangwa yoti ayikukute; ka naini pa teni, inu mukudziwa, umodzi wa mtundu umenewo. Chinthu choyamba inu mukudziwa, ndiye, ngati iye atero, iye amayendetsa zinthu kuti zizimukomera iyemwini. "Inu simungayankhule kanthu, chifukwa M'bale John Doe kumbuyo uko, ndi wothandizira chuma cha tchalitchi ichi." Mukuona? Ndiyeno inu mudzapeza Ricky wochokera ku seminare inayake, amene amadziwa zambiri za Mulungu monga momwe Nkafula amadziwira za usiku wa Aigupto, ndipo iye adzabwera pamenepo ndipo iye adzamvetsera kwa munthu ameneyo,

chifukwa iye amamugulira iye galimoto yatsopano nthawi zonse, amamulola iye azikwera pamenepo, ndipo amamugulira iye *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*.

154 Tsopano, umo ndi momwe zinayambira ndendende. Kulondola. Zindikirani, nzeru ndi kuphunzira! Iwo anati, "Tsopano taonani apa, kodi izo si za nzeru kokha? Tsopano, a . . . athu—akazi athu, zimapanga kusiyana kotani momwe iwo amavalira tsitsi lawo?" Koma Baibulo limati izo zimapanga kusiyana. Ingotengani chinthu chimodzi chimenecho, pambali pa mahandiredi a zinazo. Mukuona? Izo zimapanga kusiyana. Mulungu anati zimapanga kusiyana, kotero izo ndi zosiyana.

155 Koma, inu mukuona, ngati iwo angayambitse icho, ndi gulu la matrastii, ndi madikoni ndi chirichonse, chinthu choyamba inu mukudziwa, abusawo mwina alowamo kapena atuluka. Ndizo zonse. Mwaona, ndi anthu amene anavoteramo zimenezo. Chabwino.

156 Tsopano zindikirani, mzimu umenewo unayamba kusuntha, ndipo mpingo umene uli chomwecho, umenewo, umalemekezeka kwambiri mu zimenezo, zinthu zazikulu zambiri, ndipo ndalama zambiri zinayambika, mpaka patapita kanthawi iwo anamvetsera kwa izo ndipo anagwa chifukwa cha izo, kuyipa kwa mdierekezi.

157 Ndipo ndicho chinthu chomwecho chimene Eva anachita mmunda wa Edeni. Tsopano, inu mukuzimva zimenezo. Uko nkulondola. Taonani, mkazi wachibadwa, mkwatibwi wa Adamu, iye asanafike kwa mkaziyo monga mkazi wake, anagwera chenjerero la Satana motsutsana ndi Mawu a Mulungu, powalingalira Iwo. Adamu asanakhale naye Eva monga mkazi wake, Satana anamuposa iye pamenepo. Uko nkulondola. Inu munaumva uthenga wa *Mtengo wa Mkwatibwi,* umene ine ndinalalikira. Iwo umayankhula za izo, mwaona. Chabwino. Tsopano zindikirani, kumeneko, Eva anagwa polingalira. Tsopano iye, Satana, anayesetsa kuwalingalira Iwo.

Mkaziyo anati, "Koma Ambuye anati . . . "

158 Iye anati, "Oh, iwe ukudziwa, koma ndithudi Ambuye sangatero. Mukuona? Iwe, iwe ukufuna kukhala wanzeru. Iwe ukufuna kudziwa chinachake. Bwanji, iwe si kanthu koma mwana wopanda nzeru. Mukuona? Iwe uyenera kudziwa chinachake." Ngati uyo sali Satana! Oh, mai!

159 Ngati amenewo sali ena amakono awa, mwaona, "Oh, iwo ndi gulu chabe la oyera odzigudubuza. Musawalabadire iwo, inu mukuona. Musamapite . . . Mukuona?"

160 Tsopano, mkwatibwi wachibadwa, woyamba wa mtundu wa anthu, mwamuna wake asanafike kwa iye, iye anagwa kuchoka ku chisomo, pomvetsera kwa bodza la Satana, Mulungu atatha kumutetezera iye kuseri kwa Mawu Ake. Ngati iye akanakhala

kuseri kwa Mawu, iye sakanakhoza kugwa nkomwe. Tsopano zimenezo ndi mwathupi, zindikirani, mkazi wachibadwa.

161 Ndipo themberero lake linali chiyani, themberero lenileni la kuchoka kuseri kwa Mawu a Mulungu?

162 Tsopano kumbukirani, iye anakhulupirira pafupifupi nainte-eyiti peresenti a Iwo. Koma iwe umangoyenera kuchilola Chinthu chimodzi chichokepo. Mukuona? Iye anakhulupirira zambiri za Iwo. Oh, ndithudi. Iye ananena Ichi, ndipo Satana akanakhoza kuvomereza kuti Icho chinali cholondola. Ngati iye angakhoze kukupeza iwe pakona imodzi, ndicho chokhacho chimene iye akuchifuna. Mukuona? Chinthu chokhacho chimene iwe uyenera kuchita ndicho kupotozera chipolopolocho pang'ono mbali *iyi*, ndipo icho chidzaphonya chandamalecho. Mukuona? Ndizo zonse. Tsopano, iye anakhulupirira zochuluka kwambiri za Iwo, komabe anachiphonya icho.

163 Tsopano, ndipo—ndipo zotsatirazo, chifukwa iye anawasiya Mawu, pofuna kachidutswa kamodzi ka kulingalira.

164 Chabwino, mukuti tsopano, "Nanga bwanji za akazi?" Kapena, "Ndi chifukwa chiyani mukufuna kukamba za chinachake chonga chimenecho?" Koma chirichonse cha zinthu zazing'ono zimenezo. "Kodi pali kusiyana kotani, kaya ndi umboni woyamba?" Ndi chinachake kwa izo! Iwe uyenera . . .

165 Icho chiyenera kuwongoledwa. Ife tapenekera pa Iwo, kudutsa mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, pafupifupi. Koma ora lafika pamene Mulungu akuwayankhula Iwo. Ndipo Iye sakungowayankhula Iwo kokha, koma Iye akuwawonetsera Iwo, ndi kuwatsimikizira Iwo, ndi kuwatsimikizira Iwo. Uko nkulondola. Ngati Iye sachita zimenezo, ndiye si Mulungu, ndizo zonse. Mulungu amayima kuseri kwa Mawu Ake.

166 Zindikirani tsopano. Tsopano, mkazi wachibadwa anayambitsa imfa yachibadwa, chifukwa iye anamvetsera ku kulingalira, kuti adzipange yekha kukhala wanzeru, kudzipanga yekha kukhala wanzeru mmalo mokhala kumbuyo kwa Mawu ndi kumachita zimene Mulungu anamuuza iye kuti azichita. Iye ankafuna nzeru, ndi kukhala wanzeru. Ndipo iye anamvetsera ku kulingalira, ndipo—ndipo iye anataya mtundu wonse wa anthu. Mukuona?

167 Tsopano, nthawi iyi, mkazi wauzimu, Mkwatibwi wa Khristu amene anayamba pa Tsiku la Pentekoste, limodzi ndi Mpingo woyambirira wa atumwi, anataya chinthu chomwecho pa Msonkhano wa Nicaea. Lee, iwe ukudziwa kuti izo nzoona. Ndipo ku—ku Msonkhano waku Nicaea, pamene iye anasinthanitsa maufulu ake auzimu obadwa nawo, kuti atenge matchalitchi akuluakulu a Constantine ndi zinthu zimene iye anawapatsa iwo kumeneko, ndipo iye anagulitsa maufulu ake obadwa nawo Amalemba nkutenga mulu wa chiphunzitso Chachiroma. Tsopano, izo ndi zolimba kwa Akatolika. Koma

Achiprotestanti achita chinthu chomwecho, ndipo akuimiridwa, mu Baibulo umu, ngati mwana wamkazi "wa wachiwerewere, wa hule." Ndiko kulondola ndendende, aliyense wa iwo! Palibe zowiringula.

168 Koma kuchokera mmenemo nthawizonse mwakhala muli otsalira apang'ono, motsatira kumene, amene amapita kukapanga Mkwatibwi.

169 Zindikirani, iye anataya maufulu ake obadwa nawo, mwaona, mwamuna wake asanafike kwa iye. Mukuona? Chisanachitike chikwati, iye anataya ukoma wake.

170 Ndipo tsopano inu mukukumbukira cha uko, iye anati, "Ine ndikukhala monga mfumukazi. Ine sindisowa kanthu," mu M'badwo wa Laodikaya uwo kumeneko. "Ndine wolemera ndi wochulukidwa nacho chuma, ndi zina zotero. Ndipo, oh, dziko lonse limayang'ana kwa ine. Ndine mpingo waukulu, woyera, ndi zina zotero. Ndife anjira *iyi*," m'badwo wonsewo.

171 Ndipo Iye anati, "Iwe sukudziwa kuti ndiwe wamaliseche, wakhungu, womvetsa chisoni, watsoka, wosauka, ndipo sukudziwa izo ayi." Ndicho chikhalidwe chake. Tsopano, ngati Mzimu Woyera unati chikhalidwecho chikanadzakhala mwanjira imeneyo mmasiku otsiriza, ziri mwanjira imeneyo! Palibe njira yozilambalalira izo. Ndi momwe izo zirili.

172 Tsopano penyani. Tsopano, pamene iye anagulitsa maufulu ake obadwa nawo kumbuyo uko, ufulu wa ukoma wake, wa Mawu, kodi iye anachita chiyani? Pamene Eva anachita icho, iye anataya chirengedwe; chirengedwe chonse chinagwa pansi pa iye.

173 Tsopano zindikirani, ndipo pamene mpingo unachita chimenecho, kulandira mbalume mmalo mwa Mzimu ndi Mawu, icho chinatemberera kachitidwe konseko. Kachitidwe konse kachipembedzo kamene kanakhalapo, kapena kamene kati kadzakhalepo konse, kanatembereredwa nacho icho, ndipo kanagwa, chifukwa palibe njira yina.

174 Pamene mubweretsa gulu la amuna pamodzi, kuti achilingalire chirichonse, wina amakhala ndi lingaliro lake mwanjira *iyi*, ndipo wina amakhala ndi lingaliro lake mwanjira *iyo*, ndipo wina amakhala ndi lingaliro lake mwanjira *iyi*. Ndipo iwo amaziyika zinthuzo pamodzi ndi kudzazigwedeza izo, ndipo, pamene izo zikutuluka, ndicho chimene inu mwamupezera iye.

175 Ndicho ndendende chimene iwo anachita ku Khonsolo ya Nicene. Ndicho ndendende chimene iwo amachita ku Methodisti, Presbateria, Mpingo wa Khristu, ndi ina yonse ya iyo. Ndipo palibe munthu, ziribe kanthu kaya Mulungu awulula chiyani kwa iye, iwe umayenera kuphunzitsa izo mwanjira yomwe ziyenerezo zawo, kachikhulupiriro kawo—kachikhulupiriro kamanenera, apo ayi iwo adzakukankhira iwe

panja. Tsopano, musandiwuze ine. Ine ndakhalako kumeneko, mwaona, ndipo ine ndikuzidziwa zimenezo.

176 Ndipo ndizo ndendende basi zomwe zachitika, kotero chinthu chonsecho chatembereredwa. Nzosadabwitsa kuti mngeloyo anati, "Tulukani mwa iye, anthu Anga, kuti inu musakhale otenga nawo miliri yake." Chifukwa, iye akupita ku . . . Iye ndi wotembereredwa, ndipo iye ayenera kudzamva kuwawa kwa themberero la mkwiyo wa Mulungu pa iye, chifukwa iye anagulitsa ukoma wake ndi maufulu. Mukuona? Koma . . . Oh, mai!

177 Koma, kumbukirani. Powona chikhalidwe chonsecho, komabe Mulungu analonjeza, mu Yoweli 2:25, ngati inu mukufuna kulemba izo, "Mmasiku otsiriza . . . "

178 Pamene Iye anati, "Chimene chimbalanga chinasiya, chirimamine anachidya; chimene chirimamine anasiya, dzo—dzombe ladya; chimene dzombe linadya . . . " Basi mpaka mmusi, kachirombo pambuyo pa kachirombo, zinali zitabwera ndi kudzadya pa Mpingo umenewo mpaka potsiriza Iwo sunali kanthu koma chitsa. Penyani! Zomwe Aroma anasiya, Achilutera anadzadya; zimene Achilutera anasiya, Amethodisti anadzadya; ndipo zomwe Amethodisti anasiya, Apentekoste anadzadya; mwaona, mpaka iwo wafika pansi ku chitsa.

179 Ndipo kodi inu mukudziwa chiyani? Inu mutenge mbozi zimenezo mmenemo, dzombe ndi chirimamine, ndi zina zotero, ndipo inu muzilonde izo mmusi kudutsa mu—bukhu, ndipo mupeze. Ndi mbozi yomweyo mu masiteji osiyanasiyana chabe.

180 Gwirani mfundo yanuyo. Chomwechonso ndi Zisindikizo izi! Ndi mbozi zomwezo. Inu muziwona izo pamene ife titi tizitulutsire izo poyera, kotero ine ndikuuzani inu tsopano. Ndi mbozi yomweyo, nthawi zonse. Zinayi za mbozi zimenezo; zinayi apa. Ndipo ndi izo pamenepo, izo ndi chinthu chomwecho. Ndi mzimu womwewo. Chimene chimodzi chinasiya, chinacho chinadya; ndipo chimene *ichi* chinasiya, chinacho chinadzadya; monga choncho, mpaka izo zinawubweretsa iwo kukhala chitsa.

181 Koma Yoweli anati, "Ine ndidzabwezeretsa, atero Ambuye, zaka zonse zimene chimbalanga chinadya."

182 Ndi chiyani chimenecho? Iye achita motani zimenezo; ngati icho chinayamba, ngati wotsutsakhristu, pokhala wotsutsa kuphunzitsa kwa Khristu, amene analandira mbalume mmalo mwa Mawu? Ndipo kudutsa m'zaka okonzansowo anapenekera pa izo, monga Baibulo linanenera.

183 "Koma mu tsiku lotsiriza, pa kuwomba . . . " Chivumbulutso 10:1-7, Iye anati, "Zinsinsi za Mulungu zikanadzatsirizika mmasiku otsiriza, pa kuwomba kwa mngelo wachisanu ndi chiwiri." Malaki 4, ananena kuti Iye akanadzatero "Akanadzatumiza Eliya lisanadze tsiku loyipa pa dziko lapansi, pamene Iye adzaliwotcha ilo ngati ng'anjo. Ndipo

iye akanadzabwezeretsa, ndi kutembenuzira—ana ku Chikhulupiriro cha makolo," Chikhulupiriro chapachiyambi, chautumwi, cha Chipentekoste chinalonjezedwa kuti chidzabwezeretsedwa. Tsopano, ndizo zomveka basi monga Lemba linganenere izo. Tsopano izo zinalonjezedwa. Ndipo ngati ife tiri mmasiku otsiriza, chinachake chiyenera kuchitika. Mukuona? Ndipo izo zikuchitika, ndipo ife tikuchiwona icho.

184 Zindikirani utatu wa Satana. Munthu yemweyo akubwera; mu thupi chabe, kuchokera ku chimodzi nkudzakhala china. Umo ndi momwe zirombo zija zinachitira, mbozi zimenezo, chimodzi kwa chimzake, ndendende. Chinikolai, "wotsutsakhristu wauzimu." Papa, "mneneri wabodza." "Chirombo," mdierekezi mwiniwake, mu thupi. Iye sangakhoze kuchita zimenezo . . .

185 Tsopano, muzisunge izo mmalingaliro anu tsopano, pamene inu mukutsatira izi. Inu muwawona okwera awa akubwera kumene molunjika kwa icho. Mukuona, ine ndikukuikirani inu chithunzi apa. Ngati ndikanakhala nacho icho pa bulakibodi, inu mukanakhoza kumvetsa izo bwinoko. Mwaona, ine ndikupenyetsetsa.

186 Choyamba, tsopano. Inu mukumbukire ichi. Chinthu choyamba chimene iye ali, iye ndi "mzimu wotsutsakhristu." Yohane anatero. "Ana aang'ono, mzimu wotsutsakhristu ukugwira kale ntchito mwa ana akusamvera." Mwaona, chinthu icho chinali chitayambika. Ndiyeno icho chinadzakhala ngati "chonenedwa," mu m'badwo wa mpingo wotsatira. Ndipo m'badwo wa mpingo wotsatira, icho chinadzakhala "chiphunzitso." Ndipo m'badwo wa mpingo wotsatira, iye "anadzavekedwa korona." Tsopano kodi izo siziri zomveka basi monga kuwerenga paliponse pamene inu mungakhoze kuwerenga icho? Mukuona? Mwawona, apo iye akubwera.

187 Tsopano, poyamba, iye ankatchedwa (chiyani?) "mzimu wotsutsakhristu," chifukwa iye anali kutsutsa Mawu. Ndicho chimene chinayambitsa izo. Ndicho ndendende chimene chinachita chinthu chonsecho, kunali kuchoka ku Mawu a Mulungu. Osati chifukwa Eva mwina anamupatsa Kaini kakhofi tsiku lina. Mukuona? Icho sichinali chimene chinachita icho. Chinthu choyambirira chimene chinachita chinthu chonsecho, chinali chakuti iye anapotoloka kuchoka ku Mawu. Iye anatembenuka kuchoka ku Mawu. Ndipo chinthu choyamba, chinayambitsa uhule mu mpingo wa Mulungu wamoyo, Mkwatibwi wa Khristu, iye anapotoloka kuchoka ku Mawu ndi kulandira chiphunzitso cha Chiroma mmalo mwa Mawu a Mulungu. Chinachitika ndi chiyani kwa bungwe lirilonse? Ilo linachita chinthu chomwecho.

188 Tsopano, koma analonjeza kuti mmasiku otsiriza Iye akanadzapanga njira kuti abwezeretse kachiwiri. Mawu a

Ambuye akanadzagwera pa dziko lapansi, monga Iye anachitira izo pachiyambi, ndipo, oh, ndipo adzabwezeretsanso (chiyani?) chimene chinayambitsa izo. "Kutsutsa Mawu." Ndipo kodi munthu uyu akuyenera kudzachita chiyani pamene iye adzabwera, wodzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu? Iye basi "adzangobwezeretsa Chikhulupiriro cha ana kubwerera kwa makolo." Umo ndi momwe Iye ati adzabwezeretsere. Ndipo inu mudzawamva Mawu omwewa, mmalo omwewo amene Iwo ali *Apa*, Iwo adzachita chinthu chomwecho.

189 Yesu anati, "Ngati munthu aliyense ali wa Ine! Ndipo iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita nayenso adzazichita." Ndipo pamene iwo anamupempha Iye kuti achite zinthu zina, Iye anati, "Ine ndimangochita basi zomwe Atate andiwonetsa Ine. Ine sindimachita kanthu mpaka ine nditachiwona icho, poyamba. Chimene ine ndiwona Atate akuchichita, chimenecho inenso ndimachichita. Atate amachita ntchitoyo, ndiye kenako Ine ndimachita kuchokera pamenepo." Mukuona? Kodi inu simukuchiwona chimenecho? Bwanji, ziri ngati kuwerenga nyuzipepala. Mukuona?

Tsopano, tsopano, poyamba, ndiye, iye anadzakhala "wotsutsakhristu."

190 Tsopano, iye sakanakhoza kukhala wotsutsakhristu mu mzimu mokha. Ndiye, iye anadzakhala wotsutsakhristu, ndipo mzimu umenewo unamutenga munthu yemwe ankaphunzitsa zinthu zomwezo zimene mzimu wotsutsakhristu uwo unkachita, ndiye kenako iye anadzakhala "mneneri wabodza," kwa mzimu wotsutsakhristu. Tsopano nanga bwanji za munthu amene ali mu bungwe? Dzifanizitseni nokha. Ine sindikudziwa chimene inu mukuganiza za icho. Chabwino.

191 Tsopano, potsiriza, iye akudzakhala "chirombo." Tsopano dikirani, ndipo ife tilowa mu zimenezo pakapita kanthawi, mukuona. Chabwino.

192 Tsopano, monga utatu wa Satana ukukhala monga chomwecho; Satana, nthawi zonse. Satana, "mzimu wotsutsakhristu." Mzimu wotsutsakhristu, wosandulika thupi, "mneneri wabodza." Kenako, akudzakhala "chirombo." Mukuona? Pamene. . . Osati chiwanda, chimene chinali mwa wotsutsakhristu uyo; koma pamene Satana mwiniwake anaponyedwa kunja, iye akutsika pansi ndipo akudzatenga malowo amene panali chiwandacho. Mdierekezi, panthawiyo, kenako mdierekeziyo akudzakhala mu thupi la munthu. Izo zikungozibwereza zokha.

193 Ndicho chimene Yudasi Isikarioti anali. Ndipo kodi iye anachita chiyani? Kodi iye anali mmodzi wa anthu amene anali otsutsa Khristu? Bwanji, iye anali msungichuma, ankayenda naye Iye. Ndithudi. Ankayenda limodzi nawo iwo. Anapita

kunja uko ndipo anakatulutsako ziwanda, ndipo anakachita ndendende basi zomwe iwo ankachita.

194 Ndipo Khristu anali Mulungu mu thupi; Mulungu, atasandulika thupi, Emanuele. Ndipo Yudasi anali mwana wa chitayiko. Ndipo Yesu anali Mwana wa Mulungu. Mulungu wosandulika thupi; mdierekezi wosandulika thupi.

195 Anthu ena amangowona mitanda itatu yokha panthawi ija. Inalipo inayi ya iyo. Panali itatu pa Gologota, imene ife timayiwona. Iyo inali wa Yesu pakati, wa wakuba kumanzere Kwake, ndi wa wakuba kumanja Kwake.

196 Ndipo penyani. Wakuba mmodzi ananena kwa winayo, kapena ananena kwa Yesu, "Ngati . . . " Tsopano, inu mukudziwa Iye ndi Mawu. Koma, "Ngati iwe uli Mawu, sudzipulumutsa wekha? Suchita chinachake za chimenecho?"

197 Ndicho chinthu chomwecho lero. Kodi inu simunazimvepo ziwanda zakale izi zikubwera, nkudzati, "Ngati iwe umakhulupirira mu machiritso Auzimu, *apa* pali maso a winawake, kodi iwe sutsegula maso awo?" "Ndikanthe ine ndi khungu! Ndikanthe ine ndi khungu!" Mdierekezi wakale yemweyo. Mukuona? "Tsika pansi uchoke pa mtandapo, ife tikukhulupirira iwe." "Ngati iwe uli Mwana wa Mulungu, sandutsa miyala iyi kukhala mkate." Mdierekezi yemweyo.

198 Inu muzingochokapo, mwaona. Ayi. Umo ndi momwe Yesu ankachitira izo. Iye sanachite konse mwachisudzo kwa aliyense wa iwo.

199 Anayika chiguduli pa dzanja Lake . . . pamaso Ake ofunikirawo, monga *choncho*. Ndipo iwo anatenga ndodo, ndi kumumenya Iye pamwamba pa mutu. Anati, "Tiwuze ife! Ngati iwe uli mneneri, tsopano tiwuze ife amene wakumenya iwe." Iwo anasinthana ndodoyo, wina ndi mzake. "Tsopano tiwuze ife amene wakumenya iwe, ndipo ife tikhulupirira kuti ndiwe mneneri." Iye sanatsegule konse kamwa Yake. Iye anangokhala pamenepo. Mukuona? Iye samachita chisudzo. Iye amangochita momwe Atate akunenera, mwaona. Mukuona? Amangowalola iwo kuti azipitirira nazo. Nthawi yawo ikubwera. Musadandaule. Inde, bwana. Tsopano, iwo anakhudza chovala Chake, iwo sanamverere mphamvu.

200 Koma mkazi wamng'ono wosauka, anali nacho chosowa, anangokhudza chovala Chake. Iye anapotoloka pamenepo ndipo anati, "Ndani wandikhudza Ine?" Uh-huh. Ndi chiyani? Kukhudza kosiyana. Izo zimatengera momwe wamukhudzira Iye, inu mukuona, mwaona, chimene ukukhulupirira. Tsopano, mukuona?

201 Tsopano, pamene Satana akupita ku . . . wadzikhazika yekha mu thupi, kuchoka pokhala wotsutsakhristu nkudzakhala mneneri wabodza tsopano. Ndipo mmasiku a Myuda, ndi "wotsutsakhristu," pakati pa mpingo woyambirira. Mmibadwo

ya mdima, iye anadzakhala "mneneri wonyenga," kwa dziko. Mukumuwona iye apo ali ndi "chikho chake cha kusaeruzika"? Tsopano, ndizo kwa m'badwo wa mpingo tsopano.

202 Koma mu m'badwo uwo Mpingo utatha kupita Kwawo, iye akudzakhala chirombo, iye akudzakhala mdierekezi mu thupi, chinjoka chofiira mwiniwake. Oh, mai! Kodi simungawone chimene ine ndikutanthauza? Iye ali mwa anthu ake pamenepo. Iye ali nawo anthu ake atamangidwa ndi mphamvu yake. Mneneri wabodza wawanenera iwo mpaka mu icho. "Kuwapereka iwo ku zisokonezo zaukali, kuti akhulupirire bodza ndi kulangidwa nalo ilo." "Kumakana Mawu; ali nawo mawonekedwe aumulungu."

203 Mulungu amagwira ntchito, malo Ake, mu utatu. Kulungamitsidwa; kuyeretsedwa; ndi kudzikhazika Yekha mwa anthu Ake, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera.

204 Chinthu chomwecho, mdierekezi ali chabe mu choyimira, chotsanzira Khristu. Oh, Satana amadzikhazika yekha mu thupi . . . Tsopano yang'anani. Satana . . .

205 Pamene Yesu adzikhazika Yekha mwa anthu Ake, Moyo womwewo umene unali mwa Khristu umadzakhala mwa munthuyo.

206 Ungachite chiyani ngati inu mutachotsa moyo kuchokera mu mpesa ndi kudzawuyika iwo mu phesi la dzungu? Iwo sungabereke maungu kenanso; iwo ungabereke mphesa. Bwanji ngati inu mutatenga moyo kuchokera mu mtengo wa pichesi ndi kudzawuyika iwo mu mtengo wa peyala? Kodi iwo ungabereke mapeyala? Ayi. Ungabereke mapichesi. Moyo umanena chimene icho chiri. Mukuona?

207 Pamene inu munena kuti, ndimawamva anthu akunena kuti ali nawo Mzimu Woyera, ndi kumakana Mawu awa, apo pali chinachake cholakwika. Mzimu Woyera unalemba Mawu amenewo.

208 Ndipo Yesu ananena ichi, "Ngati munthu ali nawo Mzimu Wanga mwa iye, iye adzachita ntchito Zanga." Inu mukufuna kuziwerenga izo? Inu mukufuna kuzilemba izo? Ndi Yohane Woyera 14:12. Eya. Chabwino. "Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iye adzazichitanso. Ngakhale zochuluka kuposa izi iye adzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate." Mukuona? Ndiye Iye amamuyeretsa ndi kumutsuka iye, kuchitira kuti iye akakhoze kuima pamaso pa Mulungu. Dontho la inki lija limagwera pamenepo, ndi kumutengera iye kutsidya kwa phompholo. Mukuona?

209 Tsopano penyani. Satana, pamene iye adzikhazika yekha mwa omumvera ake, iwo amachita ntchito zimene iye ankachita. Kodi inu simukuwona? Kodi iye anachita chiyani? Anabwera kumene kwa mkazi wosalakwa uja, kudzamunyenga iye. Ndipo ndicho ndendende chimene zina za ziwanda izi zimachita, kufika

kumene pamalo ndi kumati . . . M'busa wamng'ono amayamba, cha kwinakwake; amadzalowa mkati ndi kuti, "Oh, ngati inu mutangotijowina ife!" Huh! Huh! Ntchito yomweyo ya mdierekezi. Tsopano, ndicho Choonadi! Ndipo pamene Satana analowa mu mpingo wake, kudzakhala mdierekezi, ndiye ndiwo amene amachita zaumbanda ndi kupha, ndi zina zotero. Chifukwa, Satana ndi wakupha, kuyamba ndi kuyamba; wabodza ndi . . . Mukuona? Chabwino.

210 Satana amachita chiyani pamene iye atero, pamene iye akhala mwa anthu? Ndi ntchito yake kukhala wothyathyalika. Iye ndi wothyathyalika. Inu mulifufuze Baibulo, ndipo inu mundisonyeze ine pamene Mulungu anayamba wachita nawo konse anthu anzeru. Kasakeni zimenezo, ndipo mukawone ngati si nthawizonse aluntha amene amakhala ogwidwa ndi ziwanda. Ndi mawu aakulu, koma ndi zoona. Ine ndikukutsutsani inu kuti mutenge—mzere wa mibadwo, kuchokera kwa Abele mpaka kwa Kaini; ndi, mibadwo fortini imeneyo, iyendetseni iyo, ndipo muwone amene anali ku mbali yanzeru, ndi amene anali odzichepetsa. Uh-huh.

211 Ndi chifukwa chiyani Yesu sanasankhe anthu oterowo? Iye anatenga asodzi ndi anthu amene sankakhoza ngakhale kulemba dzina lawo lomwe, kuti awayike iwo kukhala atsogoleri a Mpingo Wake. Uko nkulondola. Nzeru si—si kanthu; ndi—ndi yotsutsa Khristu. Nzeru ya chidziko imatsutsana ndi Khristu, nthawizonse. Yesu sanatiuzepo ife konse kuti tipite tizikamanga maseminare; Iye sanachitepo nkomwe zimenezo; kukhala nawo masukulu a Baibulo. Iye anati, "Kalalikireni Mawu! Kalalikireni Uthenga!" Ndiyeno ngati Iye anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira," mukuona, inu mudzayenera kukhala ndi . . . Mwa kuyankhula kwina, Iye anati, "Pitani mukawonetsere Mphamvu ya Mulungu, kwa mafuko onse."

212 Tsopano penyani. Ntchito ya Satana ndi kupotoza Mawu a Mulungu, ku kulingalira kwa nzeru. Oh, mai! Oh! Ndiye iye amawayika chizindikiro omumvera ake, pokana Mawu apachiyambi. Tsopano mulole zimenezo . . .

213 Kodi inu mutero—kodi mutero—kodi inu mupirira nane ine mowonjezera pang'ono pokha, ndi kutenga ichi? Ichi, ine sindikufuna kuti muchiphonye ichi. Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu choyimira, kuchitira kuti inu mukhoze kuchiwona icho chonse mu choyimira ndi mu Mawu, ndi chirichonse. Inu—simungakhoze . . . Inu musapite kwanu mutasokonezeka.

214 Mu Chipangano Chakale, pamene munthu wagulitsidwa ku ukapolo. Pankabwera chaka cha ufulu, zaka fifite zirizonse. Chaka cha forte-naini, ndipo kenako chaka cha ufulu. Ndipo pamene kapolo amva ichi, ndipo akafuna kuti

azipita monga mfulu, pamakhala—sipamakhala chirichose chimene chikanakhoza kumuletsa iye kuti azipita ali mfulu. Iye ankakhoza kuponyera pansi khasu lake, ndi kuti, "zatheka," nkumapita kubwerera kwawo. Lipenga lawomba. Uko nkulondola.

215 Koma ngati iye sakufuna kuti azipita, ndipo iye akukhutitsidwa naye bwana wake wa ukapoloyo, ndiye iye ankatengedwera mu—ka—kachisi, ndipo iwo ankatenga chobowolera . . . Inu mukudziwa chimene chobowolera chiri. Ndipo iwo ankakanikizira pa khutu lake, ndi kuyika bowo mu khutu lakelo. Ndipo chimakhala chizindikiro, kuti iye sangakhoze konse kubwerera kwawo. Nkulondola uko? Iye ankayenera kumamutumikira bwana uyu kwa nthawi zonse. Ine sindikusamala kaya lipenga lawufulu liwomba kangati, chirichonse chimene chingachitike. Iye mwamtheradi ankatero—ankakhala kuti wagulitsa ufulu wobadwa nawo, wa kukhala mfulu.

216 Ndipo pamene munthu akana Choonadi cha Uthenga, Satana amamuyika iye chizindikiro (pati?) pa khutu lake. Iye amamugonthetsa iye mpaka kuti iye samakhoza kumvanso Choonadi kenanso, ndipo iye watha. Iye amakhala ndi gulu lomwe iye ali nalo, ngati iye samva Choonadi. Ayi.

217 "Inu mudzadziwa Choonadi, ndipo Choonadi chidzakupangani inu mfulu." Mukuona, Choonadi chimamasula.

218 Mulungu amawayika chizindikiro Ake pamene iwo abwera. Mulungu amawayika chizindikiro Ake powatsimikizira Mawu Ake olonjezedwa kupyolera mwa iwo. Ndizo ndendende, Yohane Woyera 14:12. Ndipo chinthu china, inu mukufuna kuti muchilembe, Marko 16. Yesu anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira."

219 Tsopano tiyeni tingotenga zimenezo, miniti yokha. Kodi Iye ankaserewula? [Osonkhana akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Kodi Iye ankangotanthauza a . . . Kodi Iye ankangotanthauza atumwi, monga ena angatiwuzire ife? ["Ayi."]

220 Penyani. Kawerengeni maziko a zimenezo. "Pitani inu mpaka . . ." Kuti? [Osonkhana akuti, "Ku dziko lonse."—Mkonzi]. "Ku dziko lonse." "Kalalikireni . . . Uthenga uwu kwa . . ." Chiyani? ["Cholengedwa chirichonse."] "Cholengedwa chirichonse." Izo sizinakwaniritse nkomwe gawo limodzi mwa atatu ake panobe. "Zizindikiro izi zidzatsatira mu dziko lonse, kwa cholengedwa chirichonse, kulikonse kumene Uthenga uwu udzalalikidwa. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira," osati kwa odzaza mdzanja limodzi laling'ono okha.

221 Monga munthu wina nthawi ina anandiwuzira ine, "Mulungu anangowapatsa atumwi thwelovu aja mphatso

za machiritso. Ndipo . . . " Oh! Kotero, ambiri a abale anali atakhala pano pamene iye anadzuka kuti anene zimenezo, mwaona. Iye anapeza zokwanira za izo, mu maminiti angapo.

222 Kotero tsopano zindikirani, "Dziko lonse, kwa cholengedwa chirichonse, zizindikiro izi zidzawatsatira."

223 Musatenge chizindikiro cha kusakhulupirira cha Satana. Tsopano, iye achiyika icho pa inu usikuuno, ngati iye angakhoze kuchita zimenezo. Iye akukankhirani inu mokumenyetsani kukhoma, ndipo inu mutuluka ndi kumati, "Ine sindikudziwa za zimenezo."

224 Inu mupite kwanu ndipo mukawerenge Izo, ndipo kenako mukakhale owonamtima, ndipo mukapemphere. Chifukwa, chirichonse chiri—chiri mwangwiro kwambiri Mwamalemba pa ora lomwelino, ora lopatulika ili pa nthawiyi. Izo zakhala zikuchitika kwa zaka, kutsimikiziridwa, kubwera mpaka kwa icho. Ndipo ora lake ndi limeneli. Nthawi yake ndi imeneyi.

225 Ndipo tsopano musalole kuti iye akankhire icho ku khutu lanu, chizindikiro chake cha kusakhulupirira. Mukuona? Chifukwa, iye anali wosakhulupirira, kuyamba ndi kuyamba. Iye anawakayikira Iwo. Chabwino. Oh, musati nkomwe kuti . . . Musamulole iye kutenga Lemba, ndi nzeru zake, ndi—ndi kulipinda Ilo ndi kulipotoza Ilo ndi nzeru zake zomwe, kupita ku mphamvu za kulingalira. Inu mungokhala odzichepetsa, ndi kumati, "Mulungu ananena chomwecho, ndipo ndizo zonse ziripo kwa icho." Tsopano, oh, tiyeni . . .

226 Ife tifika pochedwa kwambiri, kotero ife kulibwino tiyimire pomwe pano ndi—ndi kuyambapo.

227 Tsopano tiyeni tipite ku Chisindikizo Chachiwiri. Pamene Mwanawankhosa wophedwa, wowuka anatsegula ichi, ndipo chachiwiri, Chamoyo chonga ng'ombe, chinati, "Bwera, udzawone chimene chinsinsi cha Chisindikizocho chiri." Mukuona? Tsopano ife tachipeza icho. Mwanawankhosa, kumbukirani, ayenera kutsegula Chisindikizo chirichonse. Ndipo Chamoyo chachiwiri . . .

228 Ngati inu munazindikira izo, mu ndondomeko ya kumene ife tangodutsa kumene, ndi mibadwo ya mpingo, chinthu chomwecho. Chachiwiri . . . Choyamba chinali mkango; chotsatira chinali—chinali . . . chinali chonga mwana wa ng'ombe, kapena ng'ombe, kapena chinachake, inu mukuona.

229 Ndipo Chamoyo ichi chinati, "Bwera, udzawone," tsopano, ndipo pamene Mwanawankhosa anatsegula Chisindikizocho. Ndipo, kenako, anapita kukawona. Ndipo pamene iye anapita mmenemo, chinachitika ndi chiyani? Tiyeni tiwone chimene iye anapeza tsopano. "Bwera, udzawone." Pali chinsinsi chosindikizidwa apa, chimene chakhala chiri pano kwa zaka thuu sauzande, pafupifupi. Tiyeni tiwone chimene icho chiri.

230 Tsopano ife tikupeza apa kuti iye anawona (chiyani?) kavalo wofiira akupita patsogolo. Tsopano, mwa kumvetsa kwanga kwa izi, mwa kumvetsa kwanga, lupanga lalikulu ili limene iye anali nalo mdzanja lake . . . Tsopano ife tiri nazo pafupifupi zinthu zitatu zoti tiziyang'anepo tsopano, kwa pafupifupi maminiti fifitini, twente. Tiyeni tingowerenga ndipo tiwone chimene Iye akunena apa. "Ndipo apo panatulukira . . . " Ndime ya 4.

> . . . *apo panatulukira kavalo wina amene anali wofiira,* (woyambayo ndi woyera): *ndipo mphamvu inapatsidwa* kwa *iye amene anakhala pamenepo kuti akachotse mtendere padziko lapansi,* . . . *kuti iwo akaphane wina ndi mzake: ndipo kunapatsidwa* kwa *iye lupanga lalikulu.*

231 Tsopano pali ziphiphiritso apa, ndipo ife tikufuna tiyang'ane pa izo mwatcheru kwenikweni. Koma, mwa kumvetsa kwanga, mopambana momwe ine ndikudziwira tsopano, inu mukuona, Yesu ananeneratu chinthu chomwecho mu Mateyu 24. Mukuona? Iye anati, "Tsopano inu mudzamva za nkhondo ndi mphekesera za nkhondo, ndipo basi nkhondo ndi mphekesera za nkhondo, ndi nkhondo. Ndipo, koma," anati, "zonse izi sizinatibe. Mukuona, nthawi sinakwanebe." Mukuona, iwo anamufunsa Yesu mafunso atatu. Mukuona? Ndipo Iye anawayankha iwo mu mafunso atatu.

232 Apo ndi pamene ambiri a abale athu anasokonezeka, kuyesera kuziyika . . . Abale a Adventist, zokhudza zimenezo, tsiku la chisanu ndi chiwiri ndi zina zotero, kumbuyo uko, a . . . "Tsoka kwa iye amene apereka mwana, amene akuyamwitsa, ndipo zipata zidzatsekedwa pa tsiku la sabata," ndi zinthu ngati zimenezo. Mai! Izo sizikugwirizana nkomwe ndi funsolo, mwaona, ayi nkomwe. Mukuona?

233 Iye anali akuyankha zimene iwo anamufunsa, koma Iye sanati—Iye sanati—sanaziyike izo zonse ku masiku otsiriza. Iye anati, "Inu mudzamva . . . " Tsopano ife tikugwira ntchito pa chinthu chimodzi ichi apa. Ife tifika kwa zochuluka zina za izo, mmausiku angapo. Penyani. Iye anati, "Inu mudzamva za nkhondo, ndi mphekesera za nkhondo, ndi zina zotero. Ndiye zonsezi siziri . . . Mwaona, kenako iwo adza—iwo adzabwereranso kachiwiri, ndiye iwo adzakuperekani inu, ndi zina zotero monga chonchi. Ndipo zonsezo, zonsezo nthawi yake siyinakwanebe."

234 Koma pamene Iye anafika ku nthawi pamene Iye anali woti ayankhule kwa iwo za zimene iwo anamufunsa Iye, "mapeto a dziko lapansi."

235 "Zidzachitika liti zinthu zonsezi, pamene sipadzakhala mwala umodzi wosiyidwapo? Chizindikiro chake chidzakhala chiyani? Ndipo adzafika liti, matsiriziro a dziko lapansi?" Mukuona, iwo anamufunsa Iye zinthu zitatu.

Ndiye pamene Iye anafika ku, “Matsiriziro a dziko lapansi?”

236 Iye anati, “Pamene mudzawone mtengo wa mkuyu ukutulutsa mphukira zake, tsopano inu mudzadziwa kuti nthawi ili pakhomo. Ndipo indetu Ine ndinena kwa inu, kuti, m’badwo uwu sudzatha mpaka zonse zitakwaniritsidwa.” Momwe wachikunja, wopanda kutanthauzira, amakondera kukhazikika pa izo! Mukuona? Iye anati, “M’badwo uwu,” osati m’badwo umene Iye anali kuyankhula nawo, “m’badwo umene unawona mtengo wa mkuyu ukutulutsa mphukira zake.”

237 Tsopano ine ndikungofuna ndikufunseni inu chinachake. Tango—tangoyang’anani pa chinachake pomwepano pa nkhope. Israeli tsopano, kwa nthawi yoyamba kwa zaka twente-faivi handiredi, fuko. Mbendera yakale kwambiri mdziko lonse ikuwuluka ku Yerusalemu usikuuno. Israeli ali ku dziko la kwawo.

238 Panali m’bale kuno nthawi yina amene ankafuna kukhala mmishonare, anamverera kuti akachite umishonare kwa Ayuda. Ine ndinati, “Iwe ukhoza kukampeza mmodzi pano ndi apo.” Oh, anthu amaganiza, fuko lonselo! Ayi, bwana.

239 Israeli amatembenuzidwa monga fuko, osati monga munthu. “Fuko lidzabadwa mu tsiku limodzi.” Ameneyo ndi Israeli. “Israeli yense ndi wopulumutsidwa.” Ingokumbukirani zimenezo. Paulo ananena chomwecho, “Israeli yense ndi wopulumutsidwa.” Tsopano zindikirani, “Israeli yense.” Ndiko kulondola ndendende.

240 Tsopano zindikirani ichi. “Koma,” Iye anati, “pamene mudzawona mtengo wa mkuyu, ndi mitengo ina yonseyo, ikuphukira masamba awo.” Tsopano penyani. Sipanakhalepo nthawi, kwa zaka twente-faivi handiredi, imene Israeli anayamba wabwerapo konse ku dziko la kwawo. Ife tiri naye kanema wamng’ono, wa *Maminiti Atatu Pasanafike Pakati Pa Usiku*, inu mukudziwa. Ndi uyo uko, fuko, mbendera ya nyenyezi ya nsonga sikisi ya Davide, ikuwuluka, ndi zinthu zonsezi.

241 Kodi inayamba yakhalapo nthawi imene zipembedzo zinakhalapo nazo konse zitsitsimutso monga izo zakhalira nazo mu zaka zingapo zapitazi? Tsopano ingophunzirani zimenezo. Ife tiri kwathu.

242 Ndi liti pamene zipembedzo zinaphukirapo konse pansi pa utumiki wa munthu aliyense, monga chachitira cha Billy Graham; Amethodisti, Abaptisti, ndi zina zotero? Ndi liti pamene kunakhalapo konse munthu, fufuzani mu mbiriyakale yanu, amene anapitapo konse kwa mpingo wamba, wokhala ndi dzina lothera ndi h-a-m, mmbuyomo? Ndikungokufunsani inu. A-b-e . . .

243 A-b-r-a-h-a-m. Tsopano penyani, dzina la Abraham liri ndi zilembo seveni, A-b-r-a-h-a-m.

244 Koma M'bale wathu Billy Graham, ali ndi G-r-a-h-a-m, sikisi, osati seveni. Dziko, ndi kumene iye akutumikirako, mpingo wathupi.

245 Mpingo wathupi, anali Loti, mu Sodomu. Ndipo pamene munthu uyu anapita kumeneko ndi kukalalikira, ndi kukawachititsa iwo khungu ndi Uthenga.

246 Koma panali Mmodzi Amene anakhala ndi Abraham, ndipo Abraham anamutcha Iye, "Elohim, Ambuye." Tsopano pamene Abraham anawona atatu akubwera, iye anati, "Ambuye wanga."

247 Pamene Loti anawona awiri akubwera, iye anati, "Azimbuye anga." Kusiyana kwake ndi kumeneko. Mukuona ntchito yanu ya utatu? Mukuona?

248 Yesu anati, "Monga zinali mmasiku a Loti." Inu mukuona zimenezo? Zindikirani. Werengetsani izo.

249 Tsopano, panali Mmodzi amene anabwera kwa Mpingo wauzimu, Mkwatibwi, Abraham, amene sanali mu—mu Sodomu, kuyamba ndi kuyamba. Ndipo penyani chimene Iye anachita. Iye sanachite kulalikira monga iwo anachitira. Iye anawaphunzitsa iwo, koma kenako iwo anawachitira iwo chizindikiro pamaso pawo. Iye anachita chizindikiro cha Umesiya. Iye anali atatembenuzira nsana Wake ku hema, ndipo Iye anati, "Abraham." Tsopano kumbukirani, dzina lake lenileni, masiku angapo zisanachitike zimenezo, linali Abram. Koma Iye anati, "Abraham, ali kuti mkazi wako, S-a-r-a-h?" Masiku angapo izo zisanachitike, ilo limatchedwa S-a-r-r-a.

Abraham anati, "Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanuko."

250 Ndipo Iye anati, "Abraham, Ine. . . " Apo pali mlowammalo wanu waumwini kenanso. "Ine ndidzakuchezera iwe molingana ndi lonjezo limene Ine ndinalipanga kwa iwe." Inu mukuona chimene icho chinali. Mukuona? Munthu, ali ndi fumbi pa zovala Zake, akudya nyama ya mwanawang'ombe, ndi kumwa mkaka kuchokera kwa ng'ombe, ndi kumadya mkate wa chimanga. Inde, bwana. Mulungu, Elohim, akuwonetseredwa mthupi!

251 Analonjeza, mmasiku otsiriza, kuti adzadziwonetsera Yekha mu thupi kachiwiri! Zindikirani.

"Abraham, ali kuti mkazi wako, Sarah?"

"Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanuko."

Anati, "Ine ndidzakuchezera iwe."

252 Ndipo donayo, zedi, pokhala wa usinkhu wa zaka handiredi, iye anakhala ngati waseka chamseri; kuseri mu hema tsopano, kuseri kwa makatani mu hema. Iye anati, "Ine, mkazi wokalamba." Chabwino, izo zinali zitasiya kukhala nawo iwo, monga mwamuna ndi mkazake, kwa zaka, inu mukudziwa, chifukwa iye anali wa zaka handiredi, ndipo—ndipo—ndipo mkaziyo anali nainte. Anati, "Zimenezo sizidzachitika konse."

253 Ndipo Iye anati, “Nchifukwa chiyani iye waseka?” Psyii! Ali ndi nsana Wake utatembenuziridwa ku hema, “Nchifukwa chiyani anaseka, kumati, ‘Zinthu izi zingachitike motani?’” Mukuona, Iye anamuwonetsera iye chizindikiro.

254 Tsopano Iye akulonjeza kuti izi zidzabwereza pa nthawi yotsiriza, kachiwiri.

255 Ndipo amuna awiriwo anatsikira kumeneko ndipo anakalalikira Mawu, ndipo anakawauza iwo kuti atuluke kumeneko; malowo anali woti awotchedwa, ndi zina zotero. Ndipo zinatero. Ndipo Loti anadzandimira kumeneko; mpingo wathupi, kumusi mu tchimo, ndi mmatope, komabe akuvutika kumeneko mu madongosolo awo achibungwe. Koma Mkwatibwi . . .

256 Munthu mmodzi uyo sanapite konse kwa iwo. Iye anangopita kokha ndi kukayitana mtundu wa Mkwatibwi. Tsopano ife tiri mmasiku otsiriza. Mukuona? Tsopano zindikirani.

“Inu munati pamenepo, ‘Mulungu, kuwonetseredwa mthupi’?”

257 Yesu anati, Mwiniwake, “Inu mukunditsutsa Ine bwanji?” Anati, “Kodi izo sizinalembedwe mu Baibulo lanu, mmalamulo anu, kuti iwo, aneneri, amene Mawu a Mulungu ankabwerako . . .” Yesu anati, “Mawu ankadza kwa aneneri,” chifukwa Iye anali Mwamalemba mu zinthu zonse. Iye anati, “Tsopano, Mawu a Mulungu amati, kuti, ‘Mawu ankadza kwa aneneri.’ Ndipo inu munkawatcha iwo ‘milungu,’ pakuti Mawu a Mulungu ankadza kwa iwo.” Anati, “Ndiye mukunditsutsa bwanji Ine pamene Ine ndikuti Ine ndine Mwana wa Mulungu?” Ndi lamulo lawo lomwe, Iye anawasoka iwo pakamwa. Ndi zimenezotu. Mukuona?

258 Tsopano ife tiri pati? Ife tiri pa nthawi yotsiriza. Tsopano mvetserani mwatcheru kwenikweni tsopano.

259 Tsopano ife tikupeza kuti kukanadzakhala nkhondo ndi mphekesera za nkhondo. Ndipo tsopano ife tikuwona kuti mtengo wa mkuyu watulutsa kale mphukira zake. Ndipo mitengo inayonso yatulutsa mphukira zake. Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, ndi onsewo, atulutsa mphukira zawo, chitsitsimutso chachikulu chikuchitika.

260 Tsopano ine ndikukhulupirira kuti Mulungu akusonkhanitsa Mkwatibwi kwa ora lotsiriza limenelo, Osankhidwawo. Oh, mai! Tsopano zindikirani.

261 Tiyeni tsopano tilingalire zimene Yohane anawona, ndiye, za zinthu izi zomwe iye anaziwona. “Kavalo wofiira; ndipo womukwera wake akutulukira, mphamvu itapatsidwa kwa iye kuti akaphe ndi lupanga lalikulu.” Tsopano apa pali vumbulutso langa la zimenezo. Uyu ndi Satana, apanso. Ndi mdierekezi, apanso, mwa mawonekedwe ena. Tsopano, ife tikudziwa kuti—

kuti Zisindikizo zinkafotokozera . . . monga ine ndinanenera usiku wina. Ndipo malipenga amafotokoza—za—za—za nkhondo yapachiweniweni, inu mukuona, pakati pa anthu, pakati pa mafuko. Koma inu mukupeza kuti, apa, kuti munthu uyu ali ndi lupanga, kotero iye akufotokoza za mpingo, nkhondo ya ndale. Tsopano inu mukhoza kusaganiza zimenezo, koma ingoyang'anani izo miniti, maminiti pang'ono chabe.

262 Zindikirani kusintha kwa mtundu wa akavalo awa. Wokwera yemweyo; kusintha kwa mtundu wa akavalo. Ndipo kavalo ndi chirombo. Ndipo chirombo, mu Baibulo, pansi pa chophiphiritsa, chimaimira mphamvu. Kachitidwe komweko kakukwera pa mtundu wina, mphamvu, kuchokera kwa woyera wosalakwa kupita kwa wamagazi wofiira. Mukuona? Muyang'aneni iye tsopano, momwe iye akubwerera.

263 Pamene iye anayamba koyambirira, iye anali basi, wabwino, iye anali chabe kachiphunzitso kakang'ono mu—mu, pakati pa anthu, kotchedwa Chinikolai. Ndithudi, iko sikakanapha chirichonse. Ndi Chivumbulutso 2:6, ngati inu mukufuna kulemba zimenezo. Iye sakanakhoza kupha chirichonse. Ndi chiphunzitso basi, mzimu chabe pakati pa anthu. Tsopano, iye sakanakhoza kupha kanthu. Oh, iye anali wosalakwa kwambiri, atakwera pa kavalo woyera uyu. "Chabwino, inu mukudziwa, ife tikhoza kukhala nawo mpingo waukulu wa dziko-lonse lapansi. Ife tikhoza kuwutcha iwo mpingo wakonsekonse." Iwo akumaterobe. Chabwino. Mukuona? Tsopano, "Ife tikhoza kukhala ndi . . . " Oh, ndi zosalakwika mwangwiro. Ndipo, oh, ndi zosalakwika kwambiri. "Ndi gulu chabe la anthu. Ife tonse tizikhala pamodzi pa chiyanjano." Mwaona, ndi zosalakwika kwambiri; ndi zoyera, kavalo woyerayo anali. Mukuona?

264 Tsopano, kotero olemekezekawo, ndi ovala bwinowo, ndi ophunzirawo, inu mukudziwa, kukhala ngati mbalame-za-nthenga zofanana, inu mukudziwa, "Titero—tizikhala ngati tikuchitira zinthu limodzi. Ndipo gulu losauka ilo, bwanji, ngati akufuna kupunthwa pamenepo, chabwino, ziri bwino, koma ife—ife—ife tipeza anthu apamwamba oti azibwera ku mpingo wathu. Ngati titati tadzichotsa apa, tidza—ife tidzakhala—ife tidzakhala gulu la a Masons, kapena zina zotero, inu mukudziwa. Tidza—ife tingokonza bwino zinthuzo, kapena, Anthu Osamvetsetseka," monga iwo aliri. Ndipo kotero ndiye . . . Osati Loji ya Anthu Osamvetsetseka tsopano, koma inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza. Kotero, ndi zosamvetsetseka kwa wokhulupirira weniweni. Tsopano, koma, mwanjirayina, mwa kuyankhula kwina, "Ife tikufuna kukhala nako kagulu kakang'ono, kachigwirizano kakang'ono kamene ife tingakhoze kukatcha kathu kathu." Icho ndi chiphunzitso basi, chosalakwa kwambiri. "Abale, bwanji, ife tiribe kanthu kokutsutsani anthu inu, ndithudi ayi. Ndinu nonse abwino, koma, inu mukudziwa, ife tikumverera kuti—kuti ife

tiri nacho chochita ndipo yense. . .Ife, tikanakhala bwinoko ngati ife titangomasonkhana limodzi." Mukuona? Izo potsiriza zinkapitirira bwino bwino mpaka zinadzachitika, inde, bwana, kubwera limodzi.

265 Koma pamene mzimu woyipa, wachinyengo uwu (oh, anthunu!) unadzalowa mu thupi, mzimu mu thupi; mzimu wa chiphunzitso uwu unadzakhala mu thupi, kuti udzatenge malo a Khristu, mwa munthu. Iwo uyenera uzipembedzedwa, ndiye, zinadzasanduka kukhala wopembedzedwa ngati Khristu. Mwa kuyankhula kwina, uko ku Vatican. . .Ine ndinafikako kumeneko. Izo zinalembedwa, "VICARIVS FILII DEI," ndipo zinalembedwa mu mawerengero Achiroma. Tsopano, inu mungojambula mzere mmusi mwa manambala Achiroma amenewo. Ndipo iwo amatanthauza "M'malo mwa Mwana wa Mulungu." Iye, mwa kuyankhula kwina, iye ndi vicar. Inu mukudziwa chimene vicar ali; wongotenga malo a chinachake. Iye ndi vicar, "Mmalo mwa Mwana wa Mulungu."

266 Ndipo Baibulo linati, "Muloleni iye amene ali nayo mphatso ya nzeru awerengere manambala a chirombo, pakuti iyo ndi nambala ya munthu. Ndipo nambala yake ndi sikisi handiredi ndi sikisite-sikisi." Tsopano, inu mutenge VICARIVS FILII DEI, ndipo mujambule mzere, ndi manambala Achiroma; "V" kukhala faivi, ndi "I" kukhala wani. . .Ndipo muziphatikizire zimenezo, ndipo muwone ngati inu simupeza sikisi handiredi ndi sikisite-sikisi.

267 Baibulo linati, "Iye akanadzakhala akukhala mu kachisi wa Mulungu, akupembedzedwa ngati Mulungu." Pamene chiphunzitso chaching'ono icho chinasandulika munthu, icho chinadzakhala vicar, "M'malo mwa Mwana wa Mulungu." Mukuona? Oh, mai! Mzimu woyipa, wachinyengo umenewo! Ngati mukufuna kuwerenga zimenezo, muwerenge mu Atesalonika Wachiwiri 2:3, ndipo inu mukhoza kuwona pamene izo ziri.

268 Ndipo, ndithudi, inu mukumbukira kuti Satana ndi mutu wa mphamvu zonse zandale, za fuko lirilonse. Ndi angati akudziwa zimenezo? Inu mukufuna kuzilemba izo? Mateyu 4:8, "Satana anamutengera Yesu pamwamba pa phiri lalitali, ndipo iye anamuwonetsa Iye maufumu onse a mdziko, amene anakhalapo konse kapena amene akanati adzakhalepo konse, mu danga la nthawi." Kunena za munthu! Iye anati, "Ine ndidzawapereka iwo kwa iwe, ngati iwe undipembedze ine." Ndipo Yesu anadziwa kuti Iye adzalandira iwo ngati cholowa chake.

269 Ndicho chimene iwo amanena, "Bwanji, inu gulu la oyera-odzigudubuza osauka!"

270 Bwanji, ife tidzalitenga dzikoli! "Ofatsa adzalandira dziko lapansi." Ndicho chimene Yesu ananena. Mukuona? Mukuona?

271 Zindikirani, Yesu ankadziwa kuti Iye akanadzalandira izo kukhala cholowa chake, kotero Iye anati, "Choka apa, Satana. Kwalembedwa," akubwereranso ndi Lemba kachiwiri, mukuona, "'Iwe udzipembedza Ambuye, ndipo Iye Yekha.'" Mukuona?

272 Tsopano—tsopano pamene—pamene iye, monga ali chiwanda chachikulu, chitasandulika thupi mwa munthu wapamwamba, wachipembedzo uyu, monga Baibulo limaneneratu, zitatero iye akulumikizitsa mpingo wake ndi boma. Mphamvu zake ziwiri zonse zikulumikizana pamodzi. Mukuona?

273 Pamene mzimu wotsutsakhristu unatulukira, iwo unali mzimu. Ndiye iwo unadzakhala chiyani? Iwo unadzakhala ndiye . . . Tsopano penyani Chisindikizo ichi. Pamene mzimuwo unapita, iwo unali wotsutsakhristu, wotsutsa chiphunzitso cha Khristu. Chabwino. Chinthu chotsatira anachita . . . Chimene Khristu anachikhazikitsa kuti Mpingo Wake uzichita, Chinali kutsutsa tchimo. "Oh, Izo sizikutanthauza zimenezo. Izo sizikutanthauza zimenezo. Izo zinali za winawake. Izo, ndi za kumbuyo uko zaka handiredi zapitazo, kumbuyo komwe. Izo, si za ife." Mukuona? Izo, mwaona, *anti*, "kutsutsa." Kenako iwo unadzakhala . . .

274 Tsopano, wokwerayo anatulukira, iye—iye analibe korona, koma iye anadzapatsidwa imodzi. Kavalo woyera ameneyo; iye anali ndi uta, wopanda mivi. Mukuona? Kotero ndiye pamene iye anapita . . .

275 Kenako, patapita kanthawi, iye anadzapatsidwa korona, chifukwa simungaveke korona pa mutu wa mzimu. Koma, pamene, mzimu uwu unadzasandulika thupi mu ntchito yachiwiri yake—ya nyengo yake ya chinsinsi chake, ntchito yachiwiri, iye anadzakhala wovekedwa korona, mneneri wabodza, ku ntchito za mzimu wotsutsakhristu. Tsopano, ife tikumuwona iye pamenepo, tsopano. Tsopano iye akudzakhala chimenecho, pamene iye akutenga icho. Ndiye, iye ali, kale, Satana akulamulira mphamvu zandale za dziko lapansi.

276 Tsopano iye akufika pamalo mpaka iye akudzapanga mphamvu ya mpingo wa konsekonse, kutenga mphamvu yachipembedzo. Ndipo kodi inu simukumvetsa, abale anga, kuti mu . . . Pamene, fuko ili likuwonekera mu mutu wa 13 wa Chivumbulutso, chinyama chaching'ono ichi chinawuka ngati mwanawankhosa. Ndipo chiri nazo nyanga ziwiri, mphamvu ya boma ndi ya chipembedzo, koma iye anachita chinthu chomwecho chimene chirombocho chinachita iye asanabwerepo.

277 Ndi zachirendo, Amerika ndi nambala sartini, ndipo mkazi. Ndi zachirendo, iye akuwoneka ngakhale mu mutu 13 wa Chivumbulutso. Ife tinayamba ndi milozo sartini mu mbendera, nyenyezi sartini. Chirichonse ndi "sartini, sartini, sartini,

sartini," njira yonse mpaka mmusi. Chirichonse ndi "mkazi, mkazi, mkazi," njira yonse mpaka mmusi.

278 Ndipo izo potsiriza zidzathera, (ine ndikuneneratu izo), mkazi adzamulamulira iye. Kumbukirani, izo zinali zaka sarte zapitazo, pamene ine ndinanena zimenezo. Ndipo—ndipo—zinthu seveni zimene ine ndinazineneratu, faivi za izo zakwaniritsidwa kale. Ndipo iwo ali naye munthuyo kumeneko tsopano kuti amubweretse mkaziyo mmenemo. Ndipo inu muvotera zimenezo, kudzera mu ndale zanu kumeneko. Eya. Huh! Chabwino.

279 Zochuluka kwambiri kuti unene, iwe sungakhoze kufika nkomwe pamene iwe ukufuna utafikapo. Zindikirani tsopano. Ine sindikusungani inu koma motalikirapo pang'ono, ngati ine ndingadzapitirizire mawa usiku.

280 Penyani. Zindikirani. Pamene Satana . . . Tsopano, aliyense, amene, akuzindikira kuti Satana akulamulira mphamvu zonse zandale za mdziko. Iye ananena chomwecho. Mateyu mutu wa 4, inu muzipeza zimenezo, ndi ndime ya 8. Maufumu onse ndi a iye. Ndi chifukwa chake iwo amamenyana, nkhondo, kupha. Tsopano kumbukirani.

281 Kodi izo si zachirendo? Iwo anapatsidwa lupanga ili, kuti aziphana wina ndi mzake. Oh, oh, oh, mai! Zindikirani tsopano.

282 Tsopano, pamene iye anachita zimenezo, iye anali asanakhale nayo mphamvu ya chipembedzo apobe. Koma iye anayamba ndi chiwanda cha chiphunzitso chabodza. Ndipo chiphunzitso chimenecho chinadzakhala chiphunzitso. Chiphunzitso chimenecho chinadzakhala mu thupi mwa mneneri wabodza.

283 Ndipo kenako iye anangopita kumalo oyenera. Iye sanapite ku Israeli, tsopano. Iye anapita ku Roma; Nicaea, Roma.

284 Msonkhanowo unachitika, ndipo iwo anasankha bishopu wamkulu. Ndiye kenako, pochita ichi, iwo analumikizitsa mpingo ndi boma pamodzi. Atatero, iye anagwetsa uta wake. Iye anatsika pakavalo wake woyera. Iye anadzakwera pa kavalo wake wofiira, kuti iye akhoze kupha aliyense yemwe sakugwirizana naye iye. Ndi chimenechotu Chisindikizo chanu. Munthu yemweyo! Muyang'aneni iye akukwerabe mpaka ku Muyaya kutaliko, limodzi naye, mwaona, walumikizitsa mphamvu zake zonsezo pamodzi.

285 Chinthu chomwecho iwo akuyesetsa kuchichita pakali pano, chinthu chomwecho, lero. Ndipo chinthu chachirendo, mwinamwake inu simukuchimvetsa icho. Koma, lero, kuchokera ku gulu la Abaptisti mu Louisville . . . Inu munazimva zimenezo pa wailesi. Woyankhula anadzuka ndipo . . . Ndi angati anamva zimenezo? Kulondola. Mukuona? Chabwino, ndi zimenezotu apa. Iwo akufuna, ndipo anafunsa mu mpingo tsopano, kuti, "Ife sitikusowa kwenikweni kutero, oh, kungokhala

ngati kujowina mpingo wa Katolika, koma ife tiyenera kumakhala ngati tikuyanjana nawo iwo." Kutenga . . . Ndipo, nthawi yomweyo imene izo zikuchitika mu Louisville, cha kuno Mulungu akufutukula Zisindikizo kwa anthu Ake, kuziwonetsa izo, "Musachite zimenezo!" Mukuwaona iwo onse akugwirira ntchito limodzi? Kumbukirani, khwangwala ndi nkhunda zinakhala pa khola limodzi, mu chombo. Ndithudi. Mungokumbukira.

286 Tsopano ife tikupeza kuti, iye akulumikizitsa mphamvu zake, pamenepo, pamene anadzakhala ziwiri zonse boma ndi mpingo, wachipembedzo. Ndiye kodi inu muchita chiyani? Iye akupanga chipembedzo chake chake. Ndipo tsopano iye akhoza kuchita chirichonse chimene iye akufuna kutero. Ndiye, iye ali nawo ufulu wopha aliyense amene sangagwirizane naye iye. Ndicho ndendende chimene iye anachita, aponso. Ndipo iye anachita zimenezo ndendende basi. Ndipo chimene iye—iye . . . Iye anachita zimenezo kwa oyera owona a Mulungu wamoyo, amene ankasunga Mawu ndipo sankagwirizana naye iye pa mbalume zake. Iye anawayika iwo ku imfa.

287 Tsopano, M'bale Lee Vayle, ndi inu aphunzitsi pano a m'badwo wa Nicaea ndi mpingo woyambirira, Ine sindikudziwa ngati inu munawerenga izi kapena ayi. Ngati inu mukufuna kukawerenga zimenezo, inu mukazipeza mu *Glorious Reformation* la Schmucker.

288 Ndipo inu mukazipeza izo, kuti, pamene Augustine Woyera waku Hippo anadzakhala wansembe pansi pa mpingo wa Chiroma, anali nawo mwayi, mpaka nthawi ina Mzimu Woyera unayesetsa kubwera pa iye, ndipo iye anawukana Iwo. Ndi angati akudziwa zimenezo, monga mphunzitsi? Chotero, iye anawukana Mzimu Woyera. Ndicho ndendende chimene, choyimira cha mpingo wa Chiprotestanti lero, umene wakana Mzimu Woyera. Iye anabwerera mpaka uko ku Hippo, ndipo iye anali yemweyo amene anakasaina zimenezo, pepala ilo limene linali ndi, "Vumbulutso lochokera kwa Mulungu, kuti zinali zabwino ndi zomkondweretsa Mulungu, kuyika munthu aliyense ku imfa amene sakhulupirira limodzi nawo mpingo wa Roma Katolika."

289 Tsopano mvetserani. Ine ndikuzitenga kuchokera mu mbiri yakale ya ofera, "Kuchokera mu nthawi ya—ya Augustine Woyera wa ku Hippo, kufikira 1586," pa za mbiriyakale ya ofera ya Chiroma, "mpingo wa Roma Katolika unawapha Achiprotestanti sikisite-eyiti millioni." Kodi lupanga lake linali lofiira? Kodi iye anali kukwera kavalo wofiira? Chinali chiyani chimenecho? Mphamvu yomweyo; wokwera yemweyo. Ndi chimenecho Chisindikizocho. Iwo amavomereza, "sikisite-eyiti millioni," pa mbiriyakale ya ofera, kupatula onse iwo amene anaphedwa kunja kwa zimenezo. Oh, chifundo! Munthawi ya mibadwo ya mdima, uko kunali mamillioni amene anadyetsedwa

kwa mikango, ndi kuphedwa mwanjira iliyonse, chifukwa iwo sankakhoza kugwadira ku mbalume iyo ya Katolika. Inu mukudziwa zimenezo.

290 Muli nayo nthawi yochuluka bwanji? [Osonkhana akuti, "Nthawi yambiri. Usiku wonse."—Mkonzi]. Chabwino. Ndiroleni ndiwerenge chinachake. Mutsegule nane ine tsopano, ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chinachake. Tiyeni—tiyeni tichijambule chinthu ichi, miniti yokha. Chinangopezeka chitabwera mmalingaliro mwanga, ndipo ife tingochiwerenga chimenecho. Tiyeni titsegule mu Chivumbulutso, ku mutu wa 17 wa Chivumbulutso. Ife tikadali nawo maminiti fifitini atsalira. Chabwino. Tsopano mvetserani kwenikweni, mwatcheru kwenikweni tsopano, pamene ife tikuwerenga. Inu amene muli ndi Mabaibulo anu ndipo mukutsegula, ine ndikupatsani inu kanthawi pang'ono kokha, kotero kuti inu mupeze pamenepo.

291 Kodi iwe unazipeza zimenezo, Lee? Mu la Schmucker ndi mmene ine ndinapezamo zimenezo, wawona, *Glorious Reform,* zimenezo zinatengedwa molunjika kuchokera mu mbiriyakale ya ofera ya Chiroma, ku Vatican.

292 Tsopano, zimenezo zinalipo mpaka kufika ku kuzunzidwa kwa anthu a Patrick Woyera. Ndiyeno iwo akumamutcha Patrick Woyera kukhala wawo—woyera wawo. Huh! Patrick Woyera anali pafupifupi Mkatolika kwambiri monga ine ndiriri; ndipo inu mukudziwa mochuluka momwe ine ndiriri. Mukuona? Iye—iye anadana nacho chiphunzitso cha mpingowo. Iye anakana kupita kwa papa. Inde, bwana. Patrick Woyera mpaka . . . Bwanji, inu, kodi inu munayamba mwapitako ku Northern Ireland, kumene iye anali nawo masukulu ake? Inu mukudziwa, dzina lake silinali Patrick. Ndi angati amadziwa zimenezo? Dzina lake linali Sucat. Ndiko kulondola. Anataya mlongo wake wamng'ono. Inu mukukumbukira pamene iwo . . . Mukuona? Chabwino.

293 Tsopano zindikirani, mutu wa 17 wa Chivumbulutso. Tsopano aliyense ingoyesetsani kuti mutsegule mtima wanu. Mulole Mzimu Woyera ukuphunzitseni inu tsopano.

> . . . *pamenepo panadza* kwa ine *mmodzi wa angelo asanu ndi awiriwo amene anali nazo—anali nazo mbale zisanu ndi ziwiri,* . . .

294 Tsopano, inu mukuona, pali Mbale Zisanu Ndi Ziwiri. Inu mukudziwa, ma seveni awa, pamene ife tikudutsamo, iwo onse akuchitika pa nthawi yomweyo; kutsatira Miliri, kutsatira mibadwo ya mpingo, mofanana basi, chifukwa izo zonse zasindikizidwa mu Bukhu limodzi limenelo, chirichonse. Ndipo chirichonse chikuchitika motsatana basi; chimodzi chikudzalowa mpaka mwa chimzake, ndipo chinacho, ndi chinacho. Pali mizimu iwiri ikugwira ntchito; Mulungu, ndi mdierekezi. Mukuona?

> . . . *amene anali nazo mbale zisanu ndi ziwiri* zotsiriza, *ndipo* iye *anayankhula nane ine, nanena . . . Bwera* kuno; ndipo ine ndikuwonetsa iwe . . . *iwe chiweruzo cha hule wamkulu amene akukhala pa madzi ambiri:*

295 Tsopano penyani apa, cha apa, amenewo, "madzi."

296 "Hule," chimenecho ndi chiyani? Ameneyo ndi mkazi. Sangakhale mwamuna. Ndipo kodi mkazi ndi chophiphiritsa cha chiyani mu mpingo, mu Baibulo? Mpingo. Bwanji? Mkwatibwi wa Khristu, ndi zina zotero; mukuona, ndiye mkazi, mpingo.

297 Tsopano, "madzi," chimenecho chikutanthauza chiyani? Yang'anani apa. Muwerenge ndime ya 15 ya izo pamenepo.

> *Ndipo iye* anati *kwa ine, Madzi amene iwe unawawona, pamene huleyo akukhala, ndi anthu, . . . unyinji, . . . mafuko, ndi malirime.*

298 Mpingo uwu unali kulamulira pa dziko lonse, mukuona, "Anakhala pa madzi ambiri."

> *Amene mafumu a dziko lapansi achita naye chiwerewere,* ziwerewere zauzimu (kutenga chiphunzitso chake, chiphunzitso cha Chinikolai), *ndipo okhala padziko lapansi aledzera naye vinyo wa* ziwerewere *zake.*

299 Mnyamata, iwe ukuyankhula za gulu loledzera, pa zimenezo! Iwe . . .

> *Kotero iye ananditengera ine kutali mu mzimu kumka mu chipululu: ndipo ine ndinamuwona mkazi . . .*

300 Ndipo kodi inu mumadziwa chiyani? Zolemba zawo zomwe za Chikatolika zimavomereza kuti uwu ndi mpingo wawo. Ndi angati amadziwa zimenezo? Mu zolemba zawo zomwe. Ine ndiri nalo bukhu la *Facts Of Our Faith*, ilo limatchedwa, tsopano, mwaona; ndi la wansembe. Chabwino. Chabwino.

> Ndipo *kotero iye ananditengera ine kutali mu mzimu kupita mu chipululu: ndipo ndinawona mkazi* atakhala *pa chirombo* chovekedwa *mtundu wofiira, chodzaza nawo maina a mwano, chakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi.*

301 Tsopano tangoyang'anani pa icho, chophiphiritsa chimenecho, imeneyo "mitu isanu ndi iwiri." Tsopano inu mukuwona apa pamene Izo zinanenedwa, "Ndipo—ndipo—ndipo . . . Mitu yomwe iwe unayiwonayo ndiyo mapiri asanu ndi awiri pamene mkaziyo akukhalapo." Roma akukhala pa mapiri asanu ndi awiri. Mukuona? Tsopano palibe cholakwika pa zimenezo, mwaona, "Mitu isanu ndi iwiri." "Ndi nyanga khumi," inu mukudziwa, ndiwo maufumu khumi, ndi zina zotero.

Ndipo mkaziyo anavala za pepo. . . zofiira,. . . wokongoletsedwa ndi golide ndi miyala ya mtengo wapatali. . . ngale, ali nacho chikho chagolide mdzanja lake chodzaza ndi zonyansa—zonyansa za *uve wa chiwerewere chake:*

302 Mzimu wotsutsakhristu umenewo, "chiwerewere," mukuona, "chiphunzitso," chimene chikuchita chigololo ndi Mulungu. Mukuona? Tsopano, iye akuyenera kukhala Mkwatibwi, mukuona; ndipo akuchita chigololo. Mukuona? Chimodzimodzi monga Eva anachitira, chimodzimodzi monga mpingo ukuchitira pamenepo. Mukuona?

Ndipo pa mutu *pake* panalembedwa, *dzina linalembedwa, CHINSINSI, BABELONI WAMKULU,. . .*

303 Ndipo aliyense amadziwa kuti, "BABELONI" ndi Roma.

. . . MAYI WA TIMAHULE NDI ZONYANSA ZA DZIKO LAPANSI.

304 Ndipo mvetserani kwa ndime ya 6.

Ndipo ine ndinamuwona mkaziyo ataledzera *nawo magazi a oyera mtima, ndipo ndi magazi a ofera a Yesu: ndipo pamene ine ndinamuwona iye, ine ndinadabwa ndi kuzizwa kwakukulu.*

305 Iye anali chinthu chokongola chomwecho, ali nayo mitanda ndi chirichonse pa iye! "Zingatheke bwanji mdziko kuti iye akakhale wolakwa pa kumwa magazi a oyera mtima?" Icho chinamudabwitsa iye. Tsopano Iye amuwuza iye.

Ndipo mngeloyo anati kwa ine, Iwe unadabwa chifukwa chiyani? Ine *ndikuwuza iwe chinsinsi cha mkaziyo, ndi. . . chirombocho chimene* chinamunyamula *iye,. . .*

306 Tsopano, izi siziri pansi pa chimodzi cha Zisindikizo. Izi ndi zinazakenso, mwaona.

Ndipo iye anati. . . *mitu isanu ndi iwiriyo ndi nyanga khumizo.*

Chirombo. . . chimene iwe unachiwonacho chinaliko, ndipo kulibe; ndipo chidzatuluka kuchokera ku phompho lopanda malire (alibe maziko, papa), *ndipo* chidza*pita mpaka ku chitayiko: ndipo iwo amene akukhala* pa *dziko lapansi adzadabwa, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo wa* Mwanawankhosa, (ndi amenewo Osankhidwawo, mwaona), *moyo kuchokera ku maziko a dziko lapansi,. . .*

307 Motani, kodi dzina lanu linaikidwa liti pa Bukhu la Moyo? Pa chitsitsimutso chija chimene inu munapitako? Ayi, bwana. "Kuchokera ku maziko a dziko lapansi."

. . . pamene iwo anawona *chirombo chimene chinaliko, . . . palibe, ndipo chiripobe.*

308 Mwaona, "chirombo," mmodzi adzafa, wina nkudzatenga malo ake. "Iye analiko; iye kunalibe. Iye analiko; iye kunalibe. Anali; iye kunalibe." Ndipo adzapita mpaka ku chitayiko, njira imeneyo. Mukuona? Chabwino.

Ndipo apa pali—ndipo apa pali lingaliro limene liri *nayo nzeru.*

309 Ndi angati akudziwa kuti pali mphatso zauzimu naini, ndipo imodzi ya izo ndi nzeru? Chabwino.

Mitu isanu ndi iwiriyo ndi mapiri asanu ndi awiri, pamene mkaziyo akukhalapo.

310 Oh, inu muyenera kukhala akhungu kwathunthu, ogontha ndi osayankhula, kuti musamvetse zimenezo. Mukuona? Chabwino.

. . . pali mafumu asanu ndi awiri: asanu anagwa, ndipo imodzi ilipo (Nero), *ndipo . . .* imodzi *ikubwera; ndipo pamene iye abwera, iye ayenera kupitiriza kwa kadanga kakafupi* chabe.

311 Inu mukukumbukira chimene iye anachita. Anawotcha mzindawo, ndipo anaziyika izo pa Akhristu. Ndipo anawayika amayi ake pa mtengo umodzi wa kavalo ndi kuwathamangitsitsa iwo kudutsa mmisewu. Ndipo anasangalala, pamene Roma ankapsya. Chabwino.

Ndipo chirombo chimene chinaliko, ndipo kulibe, ngakhale iye ndi wachisanu ndi chitatu, . . .

312 Roma wachikunja, anabweretsedwa mu Roma waupapa. Pamene mzimu wotsutsakhristu wokhala mu thupi unadzasandulika thupi, ndipo unavekedwa korona, iye anapangidwa kukhala mfumu yovekedwa korona ya Roma, monse mu boma ndi mu mpingo, limodzi. Oh, m'bale! Mwaona, zangodzaza ndi zimenezo. Mukuona?

. . . ndi . . . wachiseveni, *ndipo* iye *akupita . . .* (Akukhalapo kwa nthawi yotalika bwanji? Iwo samasintha konse kachitidweko.) . . . waku *chitayiko.*

. . . nyanga khumi unaziwonazo ndi mafumu khumi, amene sanalandire maufumu a mafumu *panobe; koma alandira mphamvu monga mafumu ora limodzi ndi chirombocho.*

313 Ndiwo olamulira mwankhanza, mukuona, ndithudi. "Awa ali nalo lingaliro limodzi." Tsopano, tayang'anani apa. Ndipo iwo akukamba za chikominisi. Mukuona?

Awa ali nalo lingaliro limodzi, ndipo adzapereka mphamvu yawo ndi nyonga kwa chirombocho.

Awa adzachita naye nkhondo Mwanawankhosa, ndipo Mwanawankhosa adzawagonjetsa iwo: pakuti iye ali Mbuye wa ambuye, *ndi Mfumu ya mafumu: ndipo iwo amene ali ndi Iye ali oyitanidwa, . . . osankhidwa, ndi okhulupirika.*

Ndipo iye anati *kwa ine, Madzi amene iwe unawawonawo, pamene huleyo wakhalapo, ali anthu, . . . makamu, . . . mafuko, ndi malirime.*

. . . nyanga khumi zimene iwe unaziwonazo pa chirombocho, izi zidzamuda huleyo, ndipo pangano limenelo laswedwa . . . (Ine ndinanena za ilo usiku wathawu.) . . . *ndipo zidzampanga iye kukhala bwinja ndi wamaliseche, ndipo zidzadya nyama yake, ndi kumuwotcha iye ndi moto.*

314 Kodi inu simukudziwa kuti Baibulo limanena kuti oyendetsa sitima zapamadzi, ndi china chirichonse, anati, "Kalanga, kalanga, mzinda waukulu uja! Momwe iwo wakumanirana nacho chiwonongeko chake mu ora limodzi!" Mukuona?

Pakuti Mulungu wayika mmitima yawo kuti akwaniritse chifuniro chake, ndi kugwirizana, ndi kuwapereka maufumu *awo kwa chirombo, kufikira* mawu *a Mulungu adzakwaniritsidwe.*

. . . mkazi amene iwe unamuwonayo ndi mzinda waukulu umenewo, umene ukulamulira pa mafumu onse *a padziko lapansi.*

315 Ndiuzeni ine umodzi. Russia sakulamulira pa onsewo. Ife sitikulamulira pa onsewo. Ilipo mfumu imodzi yokha imene imalamulira pa aliyense . . . monga chitsulo cha Nebukadinezara chikuyenderera mwa chirichonse cha zala zimenezo. Ameneyo ndi Roma. Roma samachita zimenezo monga fuko; iye amachita zimenezo monga mpingo. Fuko lirilonse pansi pa kumwamba ndi la kwa Roma.

316 Nzosadabwitsa iwo anati, "Ndani angakhoze kuchita naye nkhondo iye?" Iye akhoza kunena kuti, "Bata," [M'bale Branham anakhwatchitsa zala zake—Mkonzi]. akatero zimakhazikitsa izo. Mkatolika aliyense akati, "Basi, 'Musachite nkhondo,'" ndipo—ndipo iwo samachita nkhondo. Ndizo zonse. "Ndani ali wokhoza kuchita zimene iye angakhoze kuchita?" Palibe. Uko nkulondola. "Kotero iwo amadabwa pa zozizwitsa zimene iye akhoza kuchita." Iye akhoza kuimitsa nkhondo. [M'bale Branham anakhwatchitsa zala zake.] Chinthu chokha chimene iye ayenera kuchita ndicho kungoti, "Imani." Ndizo zonse. Koma inu mukuganiza kuti iye adzachita zimenezo? Ndithudi ayi.

317 Zindikirani, izo ndithudi zikusonyeza, "Iwo ayenera kuphana wina ndi mzake. Iwo ayenera kuphana wina ndi mzake." Uta wake unalibe mivi, poyamba, koma "lupanga lake lalikulu" linatero. Iye anadzachita kupha kwake, mtsogolo,

ndipo anasintha kuchokera ku kavalo woyera kupita ku kavalo wofiira; yemweyo, ndendende, mdierekezi, ndi lupanga lake.

318 Kodi Yesu anati chiyani? Yesu anati, "Iwo amene atenga lupanga adzawonongedwa nalo ilo." Musabwezere kumenya. Mukuona? Yesu, usiku uja pamene Iye anawauza, ananena zimenezo, ndipo Petro anatenga lupanga lake. Mukuona? Ingochitani monga Iye anachitira, zingopitirirani patsogolo.

319 Tsopano, tsopano kumbukirani, iye ali ndi lupanga. Iye akupita pamenepo, lupanga mdzanja lake; atakwera, kavalo wofiira, akuyenda kudutsa mmagazi a aliyense amene sakugwirizana naye iye.

320 Tsopano kodi mukumvetsetsa zimenezi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndi angati akumvetsa chimene Chisindikizo icho chiri tsopano? ["Ameni."] Chabwino. Tsopano, kodi Yesu ananena chiyani? "Iwo amene atenga lupanga adzawonongedwa ndi lupanga." Kodi nkulondola uko? Chabwino. Chabwino. Wokwera uyu ndi onse omumvera a ufumu wake amene akupha kudutsa mu m'badwowo, amene akhetsa magazi onse awa a ofera a oyeramtima, adzaphedwa ndi Lupanga la Yesu Khristu pamene Iye adzabwera. "Iwo amene atenga lupanga adzaphedwa ndi lupanga." Iwo anatenga lupanga la mbalume ndi wotsutsakhristu, ndi kuwadula opembedza enieni, owona, monse chotsika kudutsa mmibadwo, mpaka, chabwino, mamillioni. Ndipo pamene Khristu akubwera ndi Lupanga, pakuti ndi Mawu Ake amene akutuluka kuchokera mkamwa Mwake, Iye adzamdula mdani aliyense amene alipo patsogolo Pake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? "Kumupha mdani."

321 Tiyeni tipite cha apa miniti yokha, Chivumbulutso. Ife tiwona tsopano ngati ine ndikungonena zimenezo, kapena ngati Mawu akunena zimenezo. Chivumbulutso 19:11.

> *Ndipo ndinawona kumwamba kutatseguka* (ameni), *ndipo taonani kavalo woyera; ndipo iye amene anakhala* pa *iye akutchedwa Wokhulupirika ndi Woona, ndipo mwa chirungamo iye anaweruza ndi kuchita nkhondo.*
>
> *Maso ake anali . . .*malawi *a moto, ndipo pamutu pake . . .ma korona achifumu ambiri; . . .*

322 Oh, m'bale! Mwaona, Iye wavekedwa kale korona ndi oyera Ake, mukuona.

> *. . .ndipo iye anali nalo dzina lolembedwa, limene palibe munthu aliyense ankalidziwa, koma . . . iyemwini.*

323 Kumbukirani, ife—ife sitingakhoze, ife sitikulidziwa ilo, mukuona, chimene ilo liri. "Ndipo iye anavekedwa . . . " Tiyeni tiwone.

Ndipo iye anavekedwa ndi chovala choviikidwa mmagazi: ndipo dzina lake likutchedwa (osati "liri," koma "likutchedwa") *Mawu a Mulungu.*

324 Pakuti, Iye ndi Mawu ndi mmodzi. Mukuona? Tsopano zindikirani, osati "Maina ake." Uh-huh! "Dzina Lake likutchedwa 'Mawu a Mulungu.'" Iwo amadziwa Dzina limodzi lokha; osati dzina lina.

Ndipo ankhondo a kumwamba, *amene anali kumwamba anamutsatira iye ali pa akavalo oyera, atavala bafuta wofewa, woyera ndi waukhondo.* (Ndiko kulungama kwa oyera mtima. Mukuona?)

325 Tsopano penyani. Kodi Yesu ananena chiyani? "Iye amene atenga lupanga . . . " Chabwino, wokwera pakavalo wofiira, apa ndi pamene iye akubwera. "Iye amene atenga lupanga . . . " Inu mukhoza kukhala kuti munapha mamillioni sikisite-eyiti a iwo, mmusi kudutsa mmibadwo iyi, kuyambira nthawi imeneyo; mwinamwake ochulukirapo. Koma Yesu anati, "Iye amene atenga lupanga adzawonongedwa nalo ilo." Penyetsetsani.

Ndipo kuchokera mkamwa mwake mukutuluka lupanga lakuthwa, . . .

326 Ahebri, mutu wa 4, anati, "Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, opyoza mpaka mmafuta a mu fupa." Ndipo nchiyani chimene Iwo, Mawu, amachita? "Iwo ndi ozindikira maganizo a mu mtima." Kulondola.

. . . kuchokera mkamwa mwake munatuluka lupanga lakuthwa konsekonse *. . . lupanga lakuthwa, kuti ndi ilo iye akakanthe nalo mafuko: ndipo iye adzawalamulira iwo ndi ndodo yachitsulo: ndipo iye akuponda moponderamo mphesa wa kuwopsya kwa mkwiyo* wa *Mulungu Wamphamvuzonse.*

Ndipo iye anali nalo *pa chovala chake ndi pa ntchafu yake dzina litalembedwa, MFUMU YA* MFUMU, *NDI MBUYE WA AMBUYE.*

327 Monga otsanzira, otsutsa Mawu a Mulungu, ndipo chifukwa chakuti iwo sankavomereza, ndipo chinthu ichi . . . Satana anachikhazika, analumikizanitsa mphamvu zandale zimene iye anazigwira, ndi mphamvu zauzimu zomwe iye anazigwira, palimodzi, ndipo anapanga mpingo umene umasesa mu fuko lirilonse. Ndipo iye wayika mamillioni kuchulukitsa mamillioni . . . atatha kulumpha kuchoka pa kavalo wake woyera, nkukakwera pa kavalo wake wofiira, ndipo iye anatenga lupanga lake ndipo anapita.

328 Koma Mulungu anati, "Ndi Chinthu chomwecho chimene iye anachipotoza, kapena ankayesetsa kutero, mwa kuphunzitsa kwabodza; Mawu omwewo adzawuka mu mphamvu, akutuluka

kuchokera pa milomo ya Yesu Khristu, ndipo adzamupha iye, ndi chirichonse pamaso pa Iye." Ameni.

329 Ndi chimenecho Chisindikizo Chachiwiri. Inu mukumukonda Iye? Oh, mai! Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Matamando akhale kwa Mulungu! Ngati mavumbulutso ena onse awa, ndi masomphenya, ndi chirichonse, zagunda ndendende basi pa—pa nsonga! Ndipo ndi angati akudziwa zimenezo? Kwezani dzanja lanu. Mahandiredi, aliyense pano, manja awo ali mmwamba. Uko nkulondola. Kotero Ichinso chidzakhala! Kumbukirani, ziri chomwecho.

Oh, mzanga, bwera ku Kasupe amene wadzaza ndi Magazi,
Wotengedwa kuchokera mmitsempha ya Emmanuele,
Kumene ochimwa oponyedwa pansi pa kusefukirako,
Amataya mawanga onse a zochimwa zawo.

330 Bwerani, khulupirirani pa Iye, ngati simunatero konse. Usati utengere mwayi uliwonse; usatero, usatero, ngati pali chirichonse mmoyo wako, mzanga.

331 Ife tiri apa. Chinachake chikukonzekera kuchitika. Ine sindikudziwa chifukwa chake. Ine sindikudziwa kuti ndi liti. Ine ndikudziwa chimene chiti chichitike, koma ine sindikudziwa kuti chichitika liti. Koma icho chiyenera kutero, chifukwa Iye akuchiwulula icho pakali pano. Iye samachita chirichonse pokha Iye atachidziwitsa icho. Amosi 3. Iye amachidziwitsa icho, poyamba. Ndipo Iye analonjeza kuti zinthu izi zikanadzabwera mmasiku otsiriza. Ndipo m'badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, pa mapeto a iwo, pamene mtumikiyo wafika, pamenepo izo zikanadzakhalapo. Izo zikanadzaululidwa, Zisindikizo zomatulidwa zimenezo zidzaululidwa, ndipo ndi Izi apa. Tsopano, izo ndi mu Dzina la Ambuye. Khulupirira Izo, mzanga. Inde, bwana. Tulukani mu Babeloni!

332 Ine ndikufuna kunena chinachake ndisanatseke. Chifukwa, ine ndirinayo. . . Ine ndikungofika kumene hafu pasiti naini. Nthawiyo yangokwana pompano.

333 Billy ndi ine, pamene ife tinatsika mu ndege, mu India, ulendo wathu wotsiriza kumeneko. Ine ndinali kuyang'ana pa—pa pepala limene iwo analibweretsa, linalembedwa mu Chingerezi. Ndipo ilo linati, "Chivomezi chiyenera kuti chatha; mbalame zikubwereranso." Kenako linalongosola mwa tsatanetsatane. Iwo. . . Uko kunali chinachake choseketsa chimene chinachitika.

334 Ku India kulibe mipanda yoluka monga ife timachitira. Iwo amatola miyala, ndi kumangira mipanda yawo. Ndipo iwo amamanga nyumba zawo zambiri ndi miyala, kungoyisanja iyo pamenepo. Ndipo nkotentha kumeneko, kozungulira, oh,

paliponse, pafupifupi, mu India, kupatula ngati utakhala mmwamba mmapiri. Ndipo monse kudutsa mu Calcutta ndi zinthu, anthu amangogona mmisewu, akufa nayo njala, ndi zina zotero.

335 Tsopano, kotero, ndipo iwo amamanga nyumba zawo mu nsanja, za nyumba zawo. Iwo amadutsitsa—mpandawo mpaka cha apa, ku mbali kwa nyumba yawo. Amamanga nsanja ya nyumba yawo, ndipo nsanjayo imakhoza kukhala kumene iwo ali nacho chitsime chawo. Iwo amakumbira icho ng'ombe zawo ndi zinthu, ndiye amazungulitsa mipanda yawo konseko.

336 Ndipo, zonse mwakamodzi, chinachake chinayamba kuchitika. Mbalame zazing'ono, inu mukudziwa, zimapita mu miyala imeneyo, ndipo izo zimamanga zisa zawo ndipo zimalera ana awo. Ndipo chinachake chinayamba kuchitika.

337 Tsiku lirilonse, pamene kuyamba kutentha, ng'ombe zonse zimabwera mozungulira ndi kuyima pansi pa mthunzi wa makoma amenewo; kuti zizimva kuzizirira.

338 Ndipo mbalame zonse zazing'ono zimakhala m'malo amenewo. Ndipo, zonse mwadzidzidzi, mbalame zazing'ono zonse izo, pa chifukwa china chosadziwika . . . Tsopano, inu mukudziwa zimene ife tinanena tsiku lina zokhudza mbalame zazing'ono. Mukuona? Chifukwa china chosadziwika, izo zonse zinanyamuka. Ndipo izo zinapita kunja, ndipo sizinabwerere ku zisa zawo. Izo zinapita kunja ku minda, ndipo izo zinakatera mmitengo, ndi kulikonse kumene izo zikanakhoza kukafika, kapena pansi pamene.

339 Ng'ombezo sizinakhoze kubwera pafupi. Nkhosa sizinakhoze kubwera pafupi. Izo zinakakhala kuthengo komweko, ndipo zinatsamirana ina ndi imzake. Ndiyo njira yabwino yochitira. Izo zinadziwa kuti chinachake chinali choti chichitika.

340 Ndiye, zonse mwadzidzidzi, chivomezi chinachitika, ndipo chinagwetsera makomawo pansi, mipandayo pansi, ndi china chirichonse.

341 Kenako mbalame zazing'onozo zinayamba kubwerera. Sizinabwerere kwa masiku atatu kapena anayi; kenako zinayamba kubwerera. Iwo anati, "Chabwino, zivomezizo ziyenera kuti zatha tsopano; mbalamezo zikubwereranso."

342 Bwanji? Kodi inu simukukhulupirira kuti Mulungu yemweyo amene anakhoza kuzipangitsa mbalame izo ndi ng'ombe ndi nkhosa, mmasiku a Nowa, kukalowa mu chombo, Iye akadali Mulungu yemweyo amene angakhoze kuzipangitsa izo kuwulukira ku chitetezero? Nkulondola uko?

343 Tsopano mundirole ine ndinene chinachake, m'bale. Pali chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Ndipo makoma onse aakulu awa, akale azipembedzo adzagwa, ndipo adzabwerera

mmbuyo momwe cha kutsidyako, ndi kukagwirizana. Chifukwa, iwo adzachita zimenezo, motsimikiza monga ine ndaimira pano. Kuli "fano la chirombo chimenecho," motsimikiza basi monga ine ndaimira pano; ndipo fuko ili linachitenga icho, molingana ndi Mawu a Ambuye. Mvetserani, pamene inu mukumverera kumverera kwakung'ono, kwachirendo uko, inu muchoke ku makoma amenewo. Mupite kutali! Inu mufera mmenemo. Musachite zimenezo! Tulukani mwa izo! Chokaniko ku zinthu zonse izi! Thawirani ku chitetezero, mwamsanga momwe inu mungathere. Mupemphe chifundo kwa Mulungu.

344 Musangotenga, za ena, "Chabwino, amayi anga anali Amethodisti, kotero inenso ndikuganiza kuti ndikhala. Bambo anga anali a Baptisti; inenso ndikhala." Musachite zimenezo. Musatero inu—musati mutengere mwayi uliwonse.

345 Ine sindikusamala momwe Iwo akuwonekera mophweka ndi modzichepetsa; Iwo ndi Mawu a Ambuye. Inu muthawire kwa Yesu Khristu mwamsanga basi momwe inu mungathere, ndipo mukakhale kumeneko mpaka Mulungu atakudzazani inu ndi Mzimu Wake Woyera. Pakuti ora lidzabwera pamene inu mudzawusaka Iwo, ndipo Iwo sudzakhala ulipo. Kotero, khalani otsimikiza kuti muchite zimenezo.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu, mphindi yokha.

346 Atate Akumwamba, oh, ine—ine basi, nthawizina, Ambuye, kuyima pano ndipo—ndipo ine ndimanjenjemera. Ine ndimaganiza za ora lowopsya lija limene likuyandikira, ndipo ine. . . Palibe njira yoliyimitsira ilo. Zinanenedweratu kuti ilo lidzabwera. Ndipo ine ndinaganiza za, "Nchifukwa chiyani anthu samabwera ndi—ndi—ndi kudzamvetsera? Ndipo kodi iwo sabwera ndi kudzawulandira Iwo?" Koma, ndithudi, ine ndikudziwa kuti—kuti Inu—Inu munati iwo sakanadzakhoza, kotero iwo sadzatero.

347 Koma pali ena amene ali nawo maina awo analembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Ndipo pamene Zisindikizo zimenezo zikuponyedwa motseguka pamenepo, iwo akuwona dzina lawo pamenepo, ndipo Mzimu Woyera ukuyankhula kwa iwo. Iwo akumabwera. Iwe sungawachotsepo iwo; palibe amene angakhoze kutero, palibe aliyense. Iwo akubwera, mulimonse, chifukwa Inu mukuwatsogolera iwo monga Inu munachitira ndi mbalame zazing'ono zija, ndi nkhosa ndi ng'ombe. Inu ndinu Mulungu! Kununkhiza kwinakwake kumene zinyama zimenezo ziri nako, mwakuti izo zimadziwa kuti izo ziyenera kuthawa! Ndipo ngati kununkhiza, kwa chinyama, kungakhoze kuchichenjeza icho kuti chithawe chowopysa, Mzimu Woyera uyenera kuchita chiyani kwa Mpingo umene ukudzinenera kuti ndi wodzazidwa ndi Iwo!

348 Mulungu, mutichitire ife chifundo. Mutikhululukire ife tonse, Ambuye, chifukwa cha zolephera zathu. Ife

sitikutanthauza kuyima pa guwa ili ndi kuwalola anthu awa adzaime mozungulira makoma, ndipo miyendo yawo ikupweteka, ndiye kenako nkungopita ndi kumati, "Chabwino, izo zikumveka bwino kwambiri." Ambuye, ife tikufuna kuchita chinachake pa izo. Ife, ife tikufuna kuti Inu mufufuze mitima yathu. Ngati pali chinachake cholakwika, Ambuye, tidziwitseni ife tsopano. Chonde musatilore ife kuti tidzafike ku ora limenelo, uko, pamene nthawi idzakhala itatha. Ndifufuzeni ine. Ndiyeseni ine, Ambuye.

349 Apa, ine ndayima pano mwa chisomo cha Mulungu, nditaziwona Zisindikizo zimenezo zikumatulidwa kutsidya, ndi kubwera, kudzawauza anthu. Pamene, Inu munaneneratu kuti izo zikanadzachitika mwanjira iyi, masabata apitawo. Ndipo tsopano, Atate, apa Izo ziri, pamaso pathu pomwe.

350 Tsopano, Ambuye, ndiyeseni ine. Ndifufuzeni ine. Ndifufuzeni ine, mu mtima mwanga. Ambuye, ife sikuti . . . Ife, ife tikufuna kuti Inu muyang'ane mmiyoyo yathu. Ndipo ngati muli chinachake mmenemo, chimene sichiri bwino, ingochiyankhulani icho kwa ife, Ambuye. Ife tikufuna kuchikonza chimenecho, pakali pano; pakali pano, pamene padakali Kasupe wodzaza ndi Magazi, pamene padakali—bulitchi imene ingakhoze kutsuka machimo athu ndi kusakhulupirira. Ife tikufuna tiponyere miyoyo yathu pansi pa iyo; kusakhulupirira kwathu konse. Mulungu, tithandizeni kusakhulupirira kwathu; kuchotseni iko kwa ife, Ambuye.

351 Ife tikufuna kuti tilandire chisomo chokwatulitsa. Ife tikufuna kuti tidzakhale othekera, pamene Bingu lachinsinsi ilo lidzabingule kutsidya uko, ndipo Mpingo ukutengedwera mmwamba, ife tikufuna kuti tidzakhale okonzeka kulandira Ilo. Ambuye, perekani izi.

352 Tiyeseni ife, Ambuye, ndi Mawu Anu. Tiloleni ife tiyang'ane mwa Iwo.

353 Ndipo ngati titawona kuti talephera, ngati alipo awo pano, Ambuye, amene anabatizidwa mu maudindo, osadziwa kanthu za ubatizo weniweni, woona, mulole ine ndikhale wokhulupirika monga Paulo, pamene iye anayenda kudutsa pa gombe la kumtunda kwa Efeso, ndipo iye anawapeza ophunzira akukuwa, ndi kufuula, ndi kumakhala ndi nthawi ya ulemelero, iye anati kwa iwo, "Kodi inu munalandira, ndiye, Mzimu Woyera kuyambira pamene inu munakhulupirira?"

Iwo sankadziwa konse ngati unalipo uliwonse.

Iye anati, "Ndiye munabatizidwira ku chiyani?"

Ndipo iwo anali atabatizidwa ndi mneneri waulemelero, woyera uja, koma iwo anangobatizidwa kuloza ku kulapa.

354 Ndiye iwo anabatizidwanso, mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo Paulo anawalamulira iwo kuti abatizidwe, mobwerezanso.

355 Ambuye, mu Kuwala kwa Mawu Anu: Ine ndikulamulira munthu aliyense, amene sanabatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, kuti afulumizire ku madzi, mwamsanga, pamene inu muli nawo mwayi. Inu amene simunadzazidwe ndi Mzimu Woyera, Ine ndikukulamulirani inu, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, mugwere pa maondo anu, ndipo musadzukepo mpaka Mzimu Woyera utakuyeretsani inu kwathunthu ndi kukudzazani inu ndi chikondi ndi ubwino Wake, mpaka moyo wanu utakhutitsidwa kwambiri mu Kukhalapo kwa Mulungu kuti chikhumbo chanu chonse chikhale kumutumikira Iye, ndi kuyenda kwa Iye, ndi kumagwira naye ntchito Iye, moyo wanu wonse.

356 Perekani izi. Ine ndikupemphera kuti Mulungu akupatseni inu kulamula uku, mu Dzina la Yesu Khristu.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine

Kodi inu mukumukonda Iye kwenikweni? Tsopano kwezani manja anu mmwamba.

Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

357 Ngati pali aliyense wakhala, yemwe akumverera chosowa chake usikuuno, akumverera kuti akusowa kuti abatizidwe, kapena akusowa ubatizo wa Mzimu Woyera. Inu mukudziwa chosowa chanu; icho chawululidwa kwa inu, ndipo inu mukufuna kuti mukumbukiridwe mu pemphero. Palibe mmodzi aliyense wa ife angakhoze kuwupereka Iwo kwa inu. Oh, ife tikhoza kukubatizani inu. Koma, chinthu chokhacho, ife sitingakhoze kukupatsani inu Mzimu Woyera. Mulungu amachita zimenezo, yekha. Koma inu munachimverera chosowa chanu, kuti Mulungu akuyankhula kwa mtima wanu, kuti inu mukuwusowa Iwo, Ndipo mukufuna kuti ife tikukumbukireni inu mu pemphero. Kodi inu mungaimirire, kuchitira kuti ife tikhoze kukudziwani inu, kudziwa yemwe inu muli? Mulungu akudalitseni inu. Chosowa? Ambuye akudalitseni inu.

358 Ine ndikuganiza kuti alipo handiredi ndi fifite, mwinamwake, ayima apa. Mwinamwake ziri choncho, ngati ine ndikanakhoza kuwawona onse. Ine sindikudziwa omwe ali mzipinda, ndi kuzungulira panja, akwezera manja awo mmwamba, ndi zina zotero. Koma inu muli nacho chosowa.

Tsopano tiyeni tipemphere.

359 Tsopano, inu amene mukuwawona anthu awo amene aimirira pafupi ndi inu. Ndipo iwo ayimirira ngati mboni, pamaso pa Khristu, “Ine—ine—ine ndikukusowani Inu,

Ambuye. Ine ndikukusowani Inu. Ine—ine ndikudalira kuti ndine—ndine mmodzi wa iwo amene ati akapeze dzina langa usikuuno kuseri kwa Chisindikizo icho kutsidyako, limene linayikidwa Pamenepo kuchokera ku maziko a dziko lapansi. Chinachake chinakhudza mtima wanga, ndipo ine ndaimirira, Ambuye. Kodi ndi ine? Kodi inu mukundiyitana ine? Ine ndikufuna Inu muwululire, kwa ine, dzina langa cha Kumeneko. Ndidzazeni ine, ndipo mundisindikize ine mwa Inumwini, mwa Mzimu Woyera." Inu amene munasindikizidwa kale mkati, ine ndikufuna kuti inu muimirire. Mutembenukire kwa iwo, ndipo muyike manja anu pa iwo, kuti muwapempherere iwo. Tsopano mukhale owonamtima kotheratu.

360 Atate Akumwamba, mu Dzina la Ambuye Yesu, mulole kuti Mzimu Woyera wamphamvu usunthire pa osonkhana awa, monga mphepo yamkokomo, ndi kuyitanira kwa mtima uliwonse apa, Ambuye. Ndipo mutumize pansi ubatizo wa Mzimu Woyera, pa anthu awa.

Ndipo pali madzi akudikirira.

361 "Pamene Petro anali chiyankhulire mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo amene anamva Mawu, ndipo iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera."

63-0319 Chisindikizo Chachiwiri
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chivumbulutso Cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org